



Buku la Mphunzitsi

Nthawiyabaibulo
Kalasi Lachitatu ndi Lachinayi

Maphunziro A7 - A12

Bible Educational Services

Registered Charity UK (No 1186004)

Cholinga cha Utumiki

Kukonzera ena maphunziro a Baibulo kuti apereke choonadi cha Yesu ku m'bado otsatira pa dziko lonse lapansi.

Masomphenya a Utumiki

Kupereka ku m'bado wotsatira maphunziro okwanira, m'chiyankhulo chawo powalembera ndi kuwathandiza komanso kuthandiza anzathu ena onse odzipereka pa dziko lonse.

ZOYENERA KUDZIWA

Zomwe a Bible Educational Services amachita

A Bible Educational Services (BES UK) amasindikiza maphunziro a “Nthawiyabaibulo”, “Moyo Watsopano” ndi “Okolola” a m'Chingerezi komanso amathandiza a Postal Bible Schools ndi mabungwe ena amene amagwiritsa ntchito maphunziro a BES ku UK ndi ku mayiko a kutsidya la nyanja pokawachezera, kugwira nawo ntchito limodzi, kuwalangiza ndi kuwaphunzitsa. BES imagwiranso ntchito pamodzi ndi magulu ena amene akugwira ntchito yomasulira maphunzirowa m'ziyankhulo zawo, pomasulira, kusindikiza ndi kupereka maphunziro kwa anthu ena. Maphunzirowa amaperekedwa mwaulere kwa ophunzira onse.

Maphunziro a Nthawiyabaibulo anayamba kugwiritsidwa ntchito ku Kumpoto kwa Ireland zake 60 zapitazo. A Bible Educational Services ndi amene ali ndi udindo woyang'anira ntchito yosindikiza maphunzirowa m'Chingerezi ndi m'ziyankhulo zina zonse. Maphunziro a Nthawiyabaibulo amasindikizidwa mu A4 ndipo amathandiza ophunzira m'madera ena kuti masabata anayi aliwonse azitha kutumiza mayankho ku Postal Bible School Centre kuti akachonge. Posachedwapa, tikuyamika a bungwe la Every Home Crusade (Bungwe la Chitsistimutso) ku Belfast, anayamba kusindikiza maphunziro a miyezi isanu ndi umodzi amene amatchedwa A5. Amenewa amagwiritsidwa ntchito m'matchalichi ndi m'sukulu makamaka ku mayiko akunja kuti akhale osavuta chifukwa kumeneko njira zotumizira ndi zovuta kwambiri.

Maphunziro a BES ndi apadera kwambiri chifukwa amatha kugwiritsidwa ntchito m'nyumba kapena pa gulu (tchalichi kapena sukulu), potsatira ndondomeko imene imalola ophunzira kuphunzira kwa zaka makumi awiri. Gulu lililonse lili ndi maphunziro asanu molingana ndi zaka zawo, Amene sanayambe sukulu (Kalasi 0), zaka 5-7 (Kalasi Yoyamba), zaka 8-10 (Kalasi Yachiwiri), zaka 11-13 (Kalasi Yachitatu), zaka 14-16 (Kalasi Yachinayi). Pali ndondomeko ya kaphunzitsidwe ya zaka zitatu ya gulu lililonse molingana ndi zaka zawo. (Onani peji 4.) Magulu angathe kusintha molingana ndi kuthekera kwawo. A Bibletime Resource amapereka mpata kwa ana kuphunzira Mawu a Mulungu ndi kutha kuzindikira kufunika kwa Uthenga Wabwino pa miyoyo.

Maphunziro akupezeka m'Chingerezi pa BES website – www.besweb.com kapena kuchokera kwa Mlembi Wamkulu. Amapezekanso pa website ya ziyankhulo zina. BES ali ndi zomwe analemba zothandiza amene akufuna kugwira nawo ntchitoyi, ndipo zimenezi zilinso pa website yawo.

Keyala

International and Northern Ireland Secretary (stockist of all English lessons)

Mr S Balmer, BES Office (UK), 37a Belmore Street, Enniskillen, Northern Ireland. BT74 6AA

Phone: 00 44 286 632 2462

Email: sam@besweb.com

UK Secretary – Editorial feedback

Mr Stephen Gillham

Email: stephen.gillham@besweb.com

Web address: www.besweb.com

Email address: info@besweb.com

BUKU LA MPHUNZITSI

Poyamba, maphunziro awa anakonzedwa ndi cholinga choti akhale otumizira anthu, koma lero maphunzirowa akugwiritsidwa ntchito kwambiri pamene njira zotumizira ndi zosadalirika. M'madera ena monga ku mipingo ya ku Afrika, India ndi mayiko ena kulibe njira zotumizira zodalirika. Chifukwa cha ichi, Buku la Mphunzitsi linakonzedwa kuti lithandize amene sangathe kulandira pa positi. Buku la Mphunzitsi m'buku lino ndi la Kalasi Lachitatu ndi Lachinayi.

Buku la Mphunzitsi lililonse lili ndi ndime zonse zimene zili m'maphunziro a Nthawiyabaibulo. Maphunziro a Nthawiyabaibulo ndi Buku la Mphunzitsi zinakonzedwa kuti zigwire ntchito sabata lililonse. Maphunziro a mwezi wa Epulo amafotokoza za Paska ndipo a mwezi wa Disembala za Khirisimasi.

Madera ena amagwiritsa ntchito maphunziro a pa mwezi otchedwa A4, amene ali ndi maphunziro anayi ndipo ena amagwiritsa ntchito maphunziro otchedwa A5 amene ali ndi maphunziro 24. Mphunzitsi kapena mtsogoleri akuyenera kupereka maphunziro a A4, ndipo sabata lililonse azilemba mayankho a phunzirolo m'tchalichi, ku sukulu kapena ku nyumba ndi kupereka mayankhowo sabata lotsatiralo. Kumapeto kwa mwezi, mphunzitsi kapena mtsogoleri adzilandira maphunzirowo ndi kukachonga, akatsiriza abwere nawo ndi kupereka kwa ophunzirawo.

Ngati ophunzira akugwiritsa ntchito buku, mphunzitsi atenge bukulo kumapeto kwa phunziro lililonse ndi kukachonga. Koma tikudziwa kuti madera ena izi ndi zosatheka. Ngati akuphunzira m'kalasi, ophunzira asinthane mabuku awo ndipo mphunzitsi kapena mtsogoleri awathandize kupeza mayankho ndipo ophunzirawo achongelane maphunziro awo. Kumapeto kwa bukuli kuli malo oyika marikisi amene wophunzira wapeza mwezi uliwonse ndiponso malo a ndemanga ya mtsogoleri ya momwe wophunzirayo akuchitira m'kalasi. Palinso satifiketi yomwe wophunzira ayenera kulandira yoonetsa marikisi ake a maphunziro a miyezi isanu ndi umodzi.

Timakondwera pamene anthu akutifotokozera zomwe akukumana nazo pogwiritsa ntchito Buku la Mphunzitsi ndi mabuku a Nthawiyabaibulo ndipo tumizani ndemangazo kwa stephen.gillham@besweb.com.

KUKONZEKERA KWA APHUNZITSI

Buku la Mphunzitsi si lotsekeka kuti mphunzitsi sangathenso kuyikapo zinthu zina zomwe akuziona kuti ndi zothandiza pophunzitsa. Nawa malangizo othandiza pogwiritsa ntchito Nthawiyabaibulo.

- **Kudziwa bwino nkhani** - Aphunzitsi akuyenera kudziwa bwino nkhani ya m'Baibulo komanso phunziro la Nthawiyabaibulo lomwe akugwiritsa ntchito. Nkhani ndi yakuti, mphunzitsi awerenge phunzirolo nthawi yophunzitsa isanakwane. Iye amvetse bwino ndondomeko ya phunziro lililonse kuti akonzekere bwino kuphunzitsako.
- **Kumvetsetsa phunziro lokaphunzitsa** - Poyamba pa ndondomeko ya phunziro lililonse pali mawu akuti, "Ife tikuphunzira kuti" motsatidwa ndi zolinga ziwiri zophunzirira zomwe mwina ana angamvetse ngati mphunzitsi atafotokoza, kenaka pali gawo lotsiriza phunziro la Nthawiyabaibulo. Cholinga chophunzirira ndi kufuna kudziwa nkhaniyo, pamene chachiwiri ndi cholimbikitsa ophunzira kuti aganizire zomwe aphunzirazo ndi kuzigwiritsa ntchito pa moyo wawo. Zolinga zimenezi zikugwirizana kwambiri ndi fundo/choonadi cha m'phunzirolo ndipo aphunzitsi akuyenera kugwiritsa ntchito zimenezi kuti adziwe momwe aphunzitsira ndi zomwe ana aphunzira.
- **Mawu oyamba** - Maphunziro onse akuyamba ndi mawu akuti, "kumene kuli ana" ali ndi zomwe akukumana nazo. Pali njira zambiri zomwe tapereka zothandiza ana kutenga mbali pa zokambirana nthawi ya maphunzirowo.
- **Kuphunzitsa** - Fundo zazikulu za phunziro tapereka. Tikuyembekezera kuti aphunzitsi sadzikhalanso akumaziwerenga pamene akuphunzitsa koma kuti akhala atadziwa bwino nkhani yonse ndipo adzitha kufotokoza nkhaniyo mochititsa chidwi. Mphunzitsi ayeseke kuti ana amvetse mitu ya maphunzirowo kuchokera pa nkhani yomwe akuphunzira ndiponso awathandize kumvetsetsa zoyenera kuchita kuchokera mu nkhaniyo. Pamene m'poyenera tayeke kufotokozera bwino monga nkhani chabe. Mawu amenewa tawalemba motere: **ITALICS.**
- **Kuphunzira** - Nkhani iliyonse ili ndi Vesi Yoloweza. Malo ena muli Mavesi Oloweza awiri; taonjezera vesi ina yomwe tikuona kuti itha kukhala yothandiza kuti ana aphunzire mosavuta. Tikukhulupirira kuti ana adzaphunzira Mavesi Oloweza ndipo aziwakumbukira koterokuti adzadziwa mavesi ambiri.

- **Kutsiriza** - Kwa amene akuphunzira m'kalasi, mphunzitsi ayenera kudziwa ngati ophunzira angathe kutsiriza ntchito yawo ndiponso za thandizo lomwe likufunika kuchokera kwa mphunzitsiyo. Kwa ophunzira ena padzafunika kuti mphunzitsi aziwerenga nkhaniyo, ophunzirawo n'kumatsatira kapena kumvera. Koma enanso adzatha kuwerenga okha nkhaniyo. M'njira zonse ziwiri, ndi kofunika kuwauza malangizo okhudzana ndi mafunso. Ngati Nthawiyabaibulo sikuchitikira m'kalasi, n'kofunika kuti aphunzitsi azipezeka kuti azithandiza kuyankha mafunso osati aziyankha ngati a m'kalasi wamba. Ophunzira ayenera kumasangalala, kulimbikitsidwa ndi kuyamikiridwa pamene kuphunzira.
- **Kukumbutsana** - Zomwe zingatheke chitani, khalani ndi nthawi ya mafunso, ya masewero ndi zina zambiri. Izi zidzathandiza kuphunzira ndi kukumbukira pamtima nkhaniyo.
- **Kuonetsa** - Nthawi zina, zinthu zoti muonetse zidzakhala zovuta kuzipeza koma ngati n'kotheke yesetsani kupeza zithunzi kapena zida zina zothandiza kuti ophunzira amvetse nkhaniyo. Zinthu zimene ophunzira akuziona zimathandiza kwambiri pofotokoza nkhani. Pamene n'zotheka, pezani zithunzi kuchokera ku www.freebibleimages.org (FBI) zomwe mungathe kulandira. Kumapeto kwa Buku la Mphunzitsi kuli zina zoonjezera momwe akufotokoza kwina kumene mungapeze zithunzi za nkhani za m'Baibulo mwaulere.
- Ngati mungapeze fotokope mutha kukulitsa zithunzizo, kukhala za kalala ndi kuzigwiritsa ntchito pophunzitsa.

Nthawi ya Phunziro

- **Machitidwe.** M' buku la Mphunzitsi muli machitidwe a phunziro lililonse, koma mphunzitsi ali ndi ufulu nthawi ndi nthawi kusintha machitidwe ake.
 1. Mawu Oyamba ndi kufotokoza nkhani - mphindi 15
 2. Kuphunzitsa Vesi Yoloweza – mphindi 5 mpaka 10
 3. Kutsiriza kulemba - mphindi 20
 4. Mafunso ndi zochitika zina mpindi 5 mpaka 10.

Kumbukirani mawu ofunika awa:

“Ndiuzeni ndipo ndidzayiwala,
ndionetseni ndipo ndidzakumbukira,
loleni ndichite nawo ndipo ndidzamvetsetsa.”

Zophunzitsa Nthawiyabaibulo

	KALASI 0 (sanayambe sukulu) Kalasi Yoyamba (Zaka 5-7) Kalasi Yachiwiri (Zaka 8-10)	Kalasi Yachitatu (Zaka 11-13)	Kalasi Yachinayi (Zaka 14+)
MAPHUNZIRO A	<ol style="list-style-type: none"> 1. Chilengedwe 2. Nowa 3. Petulo 4. Petulo - Mtanda 5. Abrahamu 6. Abrahamu 7. Petulo 8. Petulo 9. Yakobo 10. Akhristu Oyambirira 11. Paulo 12. Nkhani ya Khrisimasi 	<ol style="list-style-type: none"> 1. Chilengedwe 2. Nowa 3. Petulo 4. Petulo - Mtanda 5. Petulo 6. Abrahamu 7. Yakobo 8. Pemphero 9. Paulo 10. Paulo 11. Paulo 12. Nkhani ya Khrisimasi 	<ol style="list-style-type: none"> 1. Chilengedwe ndi Kugwa 2. Zochitika Zoyamba - Genesis 3. Petulo 4. Petulo - Mtanda 5. Petulo 6. Abrahamu 7. Yakobo 8. Moyo wa Chikhristu 9. Paulo 10. Paulo 11. Paulo 12. Nkhani ya Khrisimasi
MAPHUNZIRO B	<ol style="list-style-type: none"> 1. Moyo Woyambirira wa Khristu 2. Zodabwitsa 3. Betaniya 4. Mtanda 5. Mafanizo 6. Yosefe 7. Yosefe 8. Anthu Ankumana ndi Yesu 9. Mose 10. Mose 11. Mose 12. Nkhani ya Khrisimasi 	<ol style="list-style-type: none"> 1. Mafanizo 2. Zodabwitsa 3. Betaniya 4. Mtanda 5. Akhristu Oyambirira 6. Yosefe 7. Yosefe 8. Alembi a Uthenga Wabwino 9. Mose 10. Mose 11. Mose 12. Nkhani ya Khrisimasi 	<ol style="list-style-type: none"> 1. Mafanizo 2. Zodabwitsa 3. Betaniya 4. Mtanda 5. Akhristu Oyambirira 6. Yakobo ndi Banja Lake 7. Yosefe 8. Machitidwe 2:42 - Zoyenera Kuchita 9. Mose 10. Mose 11. Lamulo 12. Nkhani ya Khrisimasi
MAPHUNZIRO C	<ol style="list-style-type: none"> 1. Danieli 2. Zodabwitsa Zina Zambiri 3. Anthu Ankumana ndi Yesu 4. Imfa ya Khristu 5. Rute ndi Samuele 6. Davide 7. Davide 8. Yoswa 9. Eliya 10. Elisa 11. Yona 12. Nkhani ya Khrisimasi 	<ol style="list-style-type: none"> 1. Danieli 2. Anthu Ankumana ndi Yesu 3. Zodabwitsa Zina Zambiri 4. Imfa ya Khristu 5. Rute 6. Samuele 7. Davide 8. Yoswa 9. Eliya 10. Elisa 11. Anthu Amene Mulungu Anawagwiritsa Ntchito - Chipangano Chakale 12. Nkhani ya Khrisimasi 	<ol style="list-style-type: none"> 1. Danieli 2. Zoyankhula za Yesu 3. Mphamvu za Ambuye 4. Imfa ya Khristu 5. Rute 6. Samuele 7. Davide 8. Yoswa 9. Eliya 10. Elisa 11. Anthu Ena a mu Chipangano Chakale 12. Nkhani ya Khrisimasi

	A7 – KALASI Lachitatu Phunziro Loyamba – Moyo wa Yakobo Mutu – Munthu wachinyengo	A7 – KALASI Lachinayi Phunziro Loyamba – Yakobo Mutu – Munthu wachinyengo
	<p>Ndime Yowerenga: <i>Genesis 25:21-34; 27:1-29</i> Vesi Yoloweza: <i>Salimo 32:1</i></p> <p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Yakobo anaputsa m'bale wake ndi kunamiza abambo ake. 2. Mulungu amatikhulukira pamene tachimwa. 3. Mulungu akufuna kudalitsa aliyense wa ife. 	<p>Ndime Yowerenga: <i>Genesis 25:19-34; 27:1-41</i> Vesi Yoloweza: <i>Aroma 5:8</i></p> <p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Yakobo anaputsa m'bale wake ndi kunamiza abambo ake. 2. Chinyengo ndi kunama zimabweretsa mavuto ndi kusakondwa. 3. Mulungu ali ndi cholinga ndi moyo wa aliyense, ngakhale moyo ngati wa Yakobo.
MAWU OYAMBA	<ul style="list-style-type: none"> • Kambiranani za tanthauzo la mayesero, ndi za nthawi imene timayesedwa kwambiri kuti tinene bodza. • Tchulani nthawi zimenezi ndi kukambirana zifukwa zomwe mumanenera bodza. • Fotokozani za kuchita nsanje ndi nthawi zomwe tingakhale ndi nsanje ndi zifukwa zake. 	<ul style="list-style-type: none"> • Ife tikuyenera kukumana ndi zotsatira za zomwe timachita. • Lumikizani zimenezi ndi moyo wanu. Chitsanzo: Kodi ndi liti lomwe inu kapena mzanu anapeza mavuto mwina ndi apolisi chifukwa cha kuba kapena kunama? • Ganizirani chifukwa chomwe tikuyenera kulangidwa tikaphwanya lamulo (tchimo).
KUTSIRIZA	<p>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</p> <p>Kambiranani ndi Kufotokoza:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Isake atapemphera, Rebeka anabereka mapasa: Esau anali wamkulu ndipo Yakobo anali wamng'ono. 2. M'banjali munali kukondera; Isake anakonda Esau amene anali mlenje pamene Rebeka anakonda Yakobo amene anakhala pa khomo. 3. <i>Fotokozani kufunika kwa udindo wa woyamba kubadwa m'chikhaliidwe cha anthu a kummawa.</i> 4. Esau anakochokera kosaka nyama ndipo anali ndi njala; Yakobo ankaphika phala lofiira, ndipo akanamupatsa m'bale wake ngati akanasinthana udindo wa woyamba kubadwa. 5. Isake atakalamba, anafuna kudalitsa mwana wake wamkulu, koma Rebeka anagwirizana ndi Yakobo zonamiza Isake amene nthawiyi sankaoonetsetsa. Esau anali kosaka nyama yoti adzapatse bambo wake, Rebeka ndi Yakobo anakonzana chakudya mofulumira ndipo Yakobo anazibisa koma anauza Isake kuti iye anali Esau, motero analandira madalitso a woyamba kubadwa kuchokera kwa bambo wake. <p>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze. Tsirizani Phunziro Loyamba.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera A – Munthu wachinyengo.</p>	<p>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</p> <p>Kambiranani ndi Kufotokoza:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Isake atapemphera, Rebeka anabereka ana aamuna amapasa; Esau anali wamkulu ndipo Yakobo anali wamng'ono. 2. M'banja m'menemu munali kukondera; Isake anakonda Esau amene anali mlenje ndipo Rebeka anakonda Yakobo amene anakhala pa khomo. 3. <i>Fotokozani kufunika kwa udindo wa mwana woyamba kubadwa m'mayiko a kummawa.</i> 4. Esau anakochokera kosaka nyama ndipo anali ndi njala; Yakobo ankaphika phala lofiira, koma akanamupatsa m'bale wakeyo ngati akanasinthana udindo wake wa woyamba kubadwa. Iye anaonetsa chinyengo chake ndi kudzikonda kwake. 5. Isake atakalamba, ankafuna kudalitsa mwana wake wamkulu, koma Rebeka ndi Yakobo anagwirizana zonamiza Isake amene pa nthawiyi sankaoonetsetsa. Esau anali kosaka nyama kuti adzapatse bambo wake, Rebeka ndi Yakobo anachita za chinyengo ndipo anapita ndi kukauza Isake kuti iye anali Esau, motero analandira madalitso a mwana woyamba kubadwa kuchokera kwa bambo wake. 6. <i>Kambiranani chitsanzo cha chinyengo ndipo fotokozani kufunika kwa kuona mtima.</i> 7. Pamene Esau anamva izi anakwiya kwambiri ndipo anapempha abambo ake kuti amudalitse koma anali atachedwa. Iye anataya udindo wake wa woyamba kubadwa ndi madalitso ake. Iye anaganiza zofuna kupha Yakobo. <p>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze. Tsirizani Phunziro Loyamba.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera A – Munthu wachinyengo.</p>
KUKUMBUTSANA	<ol style="list-style-type: none"> 1. Kambiranani za machimo amene Yakobo anachita m'phunziro lino. 2. Kodi ndi machimo ati amene ife tikuyenera kukhulukidwa? Ganizirani ngati gulu ndipo aliyense apemphere pa yekha. 3. Pangani zinthu zosiyanasiyana zomwe zisonyeze mayankho a ophunzira. 4. Ganizirani momwe mungapemphere Mulungu kapenanso anzathu ena kuti atikhulukire. Werengani <i>Salimo 32:1-5</i> kuti muthandizike. 	<ol style="list-style-type: none"> 1. Taganizani momwe Esau anamvera mu mtima mwake pamene anazindikira za chinyengo ndi bodza la m'bale wake ndi mayi wake. 2. Taganiza za nthawi imene inu munakhala pa mavuto chifukwa cha bodza kapena chinyengo ndipo mulembe njira ziwiri zomwe zidzakuthandizani kukhala moyo wabwino m'tsogolo.
KHALANI MOYO UMENEWU	<p>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli: Lembani pa pepala machimo ena amene munachita, kenaka mung'ambe ndi kuponya motaya zinyalala. Lembaniso machimo ena pa mchenga kapena pa fumbi kenaka mufufute.</p>	<p>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Taganizirani za chikonzero chimene Mulungu anali nacho pa Yakobo ndiponso chomwe ali nacho pa moyo wanu molingalira zomwe zili pa <i>Yeremiya 29:11</i>. 2. Pemphani Mulungu kuti akuonetsereni zabwino za tsogolo lanu!

	A7 – KALASI Lachitatu Phunziro Lachiwiri – Moyo wa Yakobo Mutu – Kamaloto	A7 – KALASI Lachinayi Phunziro Lachiwiri – Yakobo Mutu – Wolota
	<p>Ndime Yowerenga: <i>Genesis 27:41-46; 28:10-22</i> Vesi Yoloweza: <i>Genesis 28:16</i></p> <p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Ngakhale Yakobo anachita cholakwa, Mulungu anali naye ndipo ankamukonda kwambiri. 2. Ndi chimodzimidzi ndi ifenso lero. 	<p>Ndime Yowerenga: <i>Genesis 27:41-46; 28:1-22</i> Vesi Yoloweza: <i>Genesis 28:16</i></p> <p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Ngakhale Yakobo anakwitsa zinthu, iye anakumana ndi Mulungu m'njira zodabwitsa ndipo anamulonjeza zambiri pa moyo wake. 2. Mulungu amachita kwa ife zomwe anachitanso kwa Yakobo.
MAWU OYAMBA	<ol style="list-style-type: none"> 1. Kambiranani za momwe Mulungu akulamulira miyoyo yathu ndi kutinso lye amadziwa zonse zimene timachita! 2. Ganizirani njira zomwe Mulungu amayankhulira ndipo mukambirane ndi anzanu kuti mupeze njira zina zambiri. 3. Pemphani ophunzira kuti afotokoze njira zomwe Mulungu amatiyankhulira lero. 	<ol style="list-style-type: none"> 1. Funsani ophunzira kuti afotokoze nthawi imene anzawo okhulupirira chinthu chabwino chadzidzidzi chinawachitikira. 2. Kodi n'kofunika kuti mukhale angwiro kuti zimenezi zikuchitikireni?
KUTSIRIZA	<p>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</p> <p>Kambiranani ndi Kufotokoza:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Esau akuganizira za kupha Yakobo bambo wake akadzamwalira. Rebeka akuwuzwa Yakobo kuti apite kwa malume wake kuti akakhale kumeneko mpaka mkwiyo wa Esau utatha. 2. Isake adalitsa Yakobo ndipo anyamuka kupita ku Padani Aramu. 3. Yakobo apuma madzulo ndipo alota maloto. Iye akuona makwerero opita kumwamba. Kenaka Ambuye akuyankhula naye, akumulonjeza za dziko limene lidzakhala la banja lake ndi zakuti lye adzakhala naye pa ulendo wake. 4. Yakobo wadzuka ndipo akutchula malowo kuti Beteli kutanthauza Nyumba ya Mulungu. 5. Yakobo akuchita lumbari pamaso pa Mulungu. Ngati Mulungu adzamuyang'anira, Yakobo adzatenga Mulungu kukhala Mulungu wake! 6. <i>Pezani zomwe tikuphunzira za nthawi imene Yakobo anali nayo ku Beteli.</i> 7. <i>Kambiranani ndi kufotokoza za chikondi cha Mulungu pa Yakobo koma osati pa tchimo lake.</i> <p>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze. Tsirizani Phunziro Lachiwiri.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera A – Kamaloto.</p>	<p>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</p> <p>Kambiranani ndi Kufotokoza:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Esau akuganizira za kupha Yakobo bambo wake akadzamwalira. Rebeka akuwuzwa Yakobo kuti apite kwa malume wake kuti akakhale kumeneko mpaka mkwiyo wa Esau utatha. 2. Isake adalitsa Yakobo ndipo anyamuka kupita ku Padani Aramu. 3. Yakobo apuma madzulo ndipo alota maloto. Iye akuona makwerero opita kumwamba. Kenaka Ambuye akuyankhula naye. Akumulonjeza za dziko limene lidzakhala la banja lake ndipo lye adzakhala naye pa ulendo wake. 4. Yakobo wadzuka ndipo akutchula malowo kuti Beteli kutanthauza kuti Nyumba ya Mulungu. 5. Yakobo akuchita lumbari pamaso pa Mulungu. Ngati Mulungu adzamuyang'anira, Yakobo adzatenga Mulungu kukhala Mulungu wake! 6. <i>Kambiranani ndi kufotokoza za chikondi cha Mulungu pa Yakobo koma osati pa tchimo lake.</i> 7. <i>Kambiranani ndi kufotokoza za kudabwa kumene tingakhale nako pamene Mulungu akuchita zinthu pa miyoyo yathu.</i> <p>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze. Tsirizani Phunziro Lachiwiri.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera A – Wolota.</p>
KUKUMBUTSANA	<p>Khalani m'magulu aang'ono, tchulani malo amene munali pamene munazindikira kuti Mulungu anali nanu, pogwiritsa ntchito mawu akuti "Mulungu anali ndi ine pano." Ganizira kufunika kwa Ahebri 13:5 tsiku ndi tsiku pa moyo wanu.</p>	<ol style="list-style-type: none"> 1. Ganizirani njira zina zomwe Mulungu amayankhulira kwa anthu lero. 2. Kodi lye amachita malonjezo otani amene ali ofunika kwa ophunzira tsiku lililonse pa moyo wawo?
KHALANI MOYO UMENEWU	<p>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Kodi zinakuchitikiranipo nthawi ina kuti munachimwa koma munkadziwabe kuti Mulungu anali nanu, ndipo m'malo mwake lye anakudalitsani? 2. Kodi zimenezi zikukuchititsani kumva motani mu mtima mwanu? 3. Kodi mukuganiza kuti Mulungu angakuyankhuleni motani m'moyo wanu? 	<p>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Kodi Mulungu anayamba wakupatsani maloto? Kodi munalotapo maloto okhala ndi tanthauzo lauzimu? Nanga malotowo ankatanthauza chiyani? Kodi anathandiza motani moyo wanu? 2. <i>Pezani m'Baibulo malonjezo anayi amene Mulungu akuchita. Pempherani za zimenezi.</i> 2. Kodi tingachite chiyani kuti tionetse kuti miyoyo yathu ndi yofunika kwambiri ndipo anatipatsa ndi Mulungu?

	A7 – KALASI Lachitatu Phunziro Lachitatu – Moyo wa Yakobo Mutu – Kukhumudwitsidwa	A7 – KALASI Lachinayi Phunziro Lachitatu – Yakobo Mutu – Kukhumudwitsidwa
	<p>Ndime Yowerenga: <i>Genesis 29:1-30</i> Vesi Yoloweza: <i>Agalatiya 6:7</i></p> <p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Yakobo - Wachinyengo naye wanamizidwa! 2. Moyo uli ngati kudzala ndi kukolola. 3. Palibe lonjezo lakuti moyo udzakhala ophweka nthawi zonse. 	<p>Ndime Yowerenga: <i>Genesis 29:1-30; 31:1-21</i> Vesi Yoloweza: <i>Agalatiya 6:7</i></p> <p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Yakobo - wachinyengo naye wanamizidwa! 2. Moyo uli ngati kudzala ndi kukolola. 3. Mulungu amatanthauza chimene amayankhula. 4. Ife tichitire ena zomwe tikanafuna kuti atichitire.
MAWU OYAMBA	<ol style="list-style-type: none"> 1. Yankhulani za kudzala ndi kukolola m'minda ndipo fotokozani kuti mbewu iliyonse imene timadzala imabereka yofanana nayo. 2. Yankhulani za makhalidwe athu abwino ndi oyipa kuti ali ndi zotsatira zake. Timakolola zomwe tadzala! 3. Taganizirani za anthu lero amene anachita zoyipa ndipo analandira zotsatira zake. 	<ol style="list-style-type: none"> 1. Yankhulani za kudzala ndi kukolola m'minda ndipo fotokozani kuti mbewu iliyonse imene timadzala imabereka yofanana nayo. 2. Yankhulani za makhalidwe athu abwino ndi oyipa kuti ali ndi zotsatira zake. 3. Taonani zomwe alemba mu nyuzipepala kapena buku la miseche kuti mupeze zitsanzo za kudzala ndi kukolola ndipo mudule pomwe alembapo ndi kuzibweretsa pamodzi ndipo mulembepo mawu anu.
KUTSIRIZA	<p>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</p> <p>Kambiranani ndi Kufotokoza:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Yakobo afika ku Aramu ndipo wakumana ndi abusa amene akumwetsa madzi nkhusa zawo. 2. Rakele, msuwani wake, afika kuti amwetse nkhusa zake ndipo Yakobo amuthandiza, kenaka iye akuwuzwa abambo ake Labani kuti Yakobo wabwera. Yakobo analandiridwa m'nyumba mwawo. 3. Yakobo agwira ntchito kwa Labani ndipo alonjezedwa kuti akagwira ntchito zaka zisanu ndi ziwiri adzakwatira Rakele, amene akumukonda kwambiri. 4. Ukwati wachitika, Yakobo wazindikira kuti Labani wamunamiza ndipo wamupatsa Leya mkulu wake wa Rakele. 5. Kenaka apatsidwanso Rakele kuti akhale mkazi wake ndipo agwiranso ntchito zaka zina zisanu ndi ziwiri. 6. <i>Kambiranani momwe Yakobo wachinyengo anayamba kukolola za chinyengo chomwe anachita zaka zam'mbuyo kwawo.</i> 7. <i>Kambiranani za njira zina zomwe anthu amathetsera kukhumudwitsidwa kwawo.</i> <p>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze. Tsirizani Phunziro Lachitatu.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera A – Kukhumudwitsidwa.</p>	<p>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</p> <p>Kambiranani ndi Kufotokoza:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Yakobo afika ku Aramu ndipo wakumana ndi abusa amene akumwetsa madzi nkhusa zawo. 2. Rakele, msuwani wake, afika kuti amwetse nkhusa zake ndipo Yakobo amuthandiza, kenaka iye akuwuzwa abambo ake Labani kuti Yakobo wabwera. Yakobo analandiridwa m'nyumba mwawo. 3. Yakobo agwira ntchito kwa Labani ndipo alonjezedwa kuti akagwira ntchito zaka zisanu ndi ziwiri adzakwatira Rakele, amene akumukonda kwambiri. 4. Ukwati wachitika, Yakobo wazindikira kuti Labani wamunamiza ndipo wamupatsa Leya mkulu wake wa Rakele. 5. Kenaka apatsidwanso Rakele kuti akhale mkazi wake ndipo agwiranso ntchito zaka zina zisanu ndi ziwiri. 6. <i>Kambiranani momwe Yakobo wachinyengo anayamba kukolola za chinyengo chomwe anachita zaka zam'mbuyo kwawo.</i> 7. Patapita nthawi Mulungu anawuzwa Yakobo kuti abwerere kwawo. Mulungu anamudalitsa ndipo anali ndi zinthu zambiri ndiponso banja lalikulu. Iye sakuwuzwa Labani kuti akupita kwawo, koma akuthawa Labani atachoka. 8. <i>Taganizani zolephera za Yakobo ndipo kambiranani momwe Mulungu amagwirira ntchito m'miyoyo yathu yosalungamayi.</i> <p>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze. Tsirizani Phunziro Lachitatu.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera A – Kukhumudwitsidwa.</p>
KUKUMBUTSANA	<p>Sankhani chitsanzo chimodzi kuchokera pa nambala 7 pamwambapa ndipo lembani pa chipepala chachikulu cha m'kalasi kuti aliyense athe kuona zomwe aliyense walembe (ngati zilipo zolembe kale, matani pa pepala).</p>	<p>Ganizirani zitsanzo za kudzala ndi kukolola m'miyoyo ya anthu, choyamba zokolola zoyipa kenaka zabwino. Lembani zomwe mwapeza ndipo zikhale zitsanzo ziwiriziwiri.</p>
KHALANI MOYO UMENEWU	<p>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Kodi ndi liti lomwe munakhumudwitsidwa? 2. Nanga munathetsa motani kukhumudwa kumeneko? 3. Kodi ilipo njira ina yabwino yomwe mukanatsatira pothetsa kukhumudwako? 4. Lembani zitsanzo zitatu za kudzala ndi kukolola m'magawo awiriwa. 	<p>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Kodi mukudziwa munthu wachinyengo amene nayenso ananamizidwa? 2. Kodi mungaganize za chitsanzo china cha khalidwe loyipa lomwe limamubwerera munthu patapita nthawi?

	A7 – KALASI Lachitatu Phunziro Lachinayi – Moyo wa Yakobo Mutu – Kuzindikira kwake	A7 – KALASI Lachinayi Phunziro Lachinayi – Yakobo Mutu – Kuzindikira
	<p>Ndime Yowerenga: <i>Genesis 32:1-21; 33:1-11</i> Vesi Yoloweza: <i>1 Yohane 1:9</i></p> <p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Ndi thandizo la Mulungu ndi zotheka kukhululukira anthu zoyipa zomwe anatichitira, monga zinachitikira ndi Yakobo. 2. Nthawi zonse Mulungu amatikhululukira pamene talapa ndi kupempha kuti atero. 	<p>Ndime Yowerenga: <i>Genesis 32:1-32; Genesis 33:1-17</i> Vesi Yoloweza: <i>1 Yohane 1:9</i></p> <p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Moyo wa Yakobo wafika povuta tsopano ndipo ndi kofunika kwambiri kuti akumane ndi Mulungu m'malo mwa m'bale wakeyo. 2. Ngakhale tsopano ndi munthu wamkulu, Mulungu anali ndi chikonzero chatsopano pa moyo wa Yakobo.
MAWU OYAMBA	<ol style="list-style-type: none"> 1. Kumbutsani ophunzira kuti Yakobo wamvera Mulungu ndipo akubwerera kwawo, koma ali ndi nkawa chifukwa cha Esau amene zaka za m'mbuyomo anamuwuza kuti adzamupha. 2. Ganizirani ngati Esau angakhululukire Yakobo. 3. Lembani zinthu zina zomwe zimakuchitikirani inuyo: a) simunakhululuke ndi b) munakhululuka. 	<ol style="list-style-type: none"> 1. Fotokozani zomwe zimachitika mukakumana ndi munthu wofunika kwambiri, ndi momwe mungakonzekere kuti mukumane naye. 2. Patapita zaka asanayankhulane ndi Mulungu, pano tsopano Yakobo akukumana ndi Mulungu. Yakobo anasinthika kwambiri ndipo Mulungu anamuthandiza kuti akakumane ndi Esau. 3. Ngati ndi zotheka pezani buku ili pa neti "The End of the Spear" kapena DVD ya mkazi wa Jim Elliott yofotokoza momwe iye anakhululukira amene anapha mwamuna wake.
KUTSIRIZA	<p>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</p> <p>Kambiranani ndi Kufotokoza:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Pezani zifukwa zomwe zinachititsa Yakobo kuti akhale ndi mantha pamene ankabwerera kwawo patapita zaka zambiri. 2. Yakobo anachita mantha kwambiri pamene anamva kuti Esau akubwera ndi anthu mazana anayi kudzakumana naye. 3. Yakobo akuchita zinthu zitatu: 1) Akugawa banja lake m'magulu awiri ndi maganizo akuti mwina gulu limodzi lidzapulumuka. (32:7-8) 2) Iye akupemphera. (32:9-12) 3) Iye akutumiza mphatso kwa Esau. (32:13-16) 4. Usiku umenewo Yakobo anakumana ndi Mulungu mwachilendo ndipo anapempha kuti amudalitse. (32:22-31) 5. Mantha a Yakobo anali opanda pake. Esau anamukhumbatira ndipo zinaoneka kuti anamukhululukira kale. Yakobo anaonetsa banja lake kwa Esau ndipo anapempha Esau kuti alandire mphatso zake. 6. Koma iye nthawi yomweyo sanapite kwa abambo wake koma ananamizanso Esau. 7. <i>Pezani zifukwa zomwe zinachititsa kuti Yakobo akayikire ndi kusavomereza malonjezo a Mulungu.</i> 8. <i>Kambiranani za kuchita mantha ndipo fotokozani kuti si zonse zimene timaziopa zimatichitikira, ngakhale timakhala nthawi zambiri tikulingalira za zimenezo.</i> <p>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze. Tsirizani Phunziro Lachinayi.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera A – Kuzindikira kwake.</p>	<p>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</p> <p>Kambiranani ndi Kufotokoza:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Pezani zifukwa zomwe zinachititsa Yakobo kuti akhale ndi mantha pamene ankabwerera kwawo patapita zaka zambiri. 2. Yakobo anachita mantha kwambiri pamene anamva kuti Esau akubwera ndi anthu mazana anayi kudzakumana naye. 3. Yakobo akuchita zinthu zitatu: 1) Akugawa banja lake m'magulu awiri ndi maganizo akuti mwina gulu limodzi lidzapulumuka. (32:7-8) 2) Iye akupemphera. (32:9-12) 3) Iye akutumiza mphatso kwa Esau. (32:13-16) 4. Usiku umenewo Yakobo anakumana ndi Mulungu mwachilendo ndipo anapempha kuti amudalitse. 5. Mantha a Yakobo anali opanda pake. Esau anamukhumbatira ndipo zinaoneka kuti anamukhululukira kale. Yakobo anaonetsa banja lake kwa Esau ndipo anapempha Esau kuti alandire mphatso zake. 6. Koma iye nthawi yomweyo sanapite kwa abambo wake ndipo ananamizanso Esau. 7. <i>Pezani zifukwa zomwe zinachititsa kuti Yakobo akayikire ndi kusavomereza malonjezo a Mulungu.</i> 8. <i>Pezani nkhani zenizeni za anthu amene anakhululukira ena.</i> 9. <i>Ganizirani mavuto amene timabweretsa pa moyo wathu ndi pa moyo wa ena ngati ife sitikhululukira.</i> <p>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze. Tsirizani Phunziro Lachinayi.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera A – Kuzindikira.</p>
KUKUMBUTSANA	<p>Molingalira zomwe taphunzirazi, lemberani kalata kwa Mulungu yofotokoza maganizo anu. Funsani ophunzira kuti aganizire zomwe akuyenera kuulula pamaso pa Mulungu, ndi zomwe angapempho ndi kuyamikanso nazo Mulungu.</p>	<p>Ganizirani za tanthauzo la kukumana ndi Mulungu</p> <ol style="list-style-type: none"> a) Kodi tingakumane naye liti? b) Kodi tingakumane naye motani? c) N'chifukwa chiyani tikuyenera kukumana naye? <p>Funsani ophunzira ngati anali ndi nthawi imene aliyense pa yekha anakumana ndi Mulungu.</p>
KHALANI MOYO UMENEWO	<p>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Kodi ndi chiyani chomwe tingaphunzire pa ndime yathu yowerenga zokhudza miyoyo yathu? 2. Perekani zitsanzo za wina amene wakhululukidwa posachedwapa. 3. Pemphani Mulungu kuti akuthandizeni kukhululukira munthu wina? 	<p>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Funsani ophunzira ngati alipo wina m'moyo wawo amene anakana kuwakhululukira kapena anawakhululukira. 2. Kodi iwo anamva bwanji mu mtima mwawo? 3. Kodi alipo amene akuyenera kumkhululukira?

	A8 – KALASI Lachitatu Phunziro Loyamba – Pemphero Mutu – Pemphero ndi chiyani?	A8 – KALASI Lachinayi Phunziro Loyamba – Kukhala Mkhristu Mutu – Kuphunzira za pemphero
	<p>Ndime Yowerenga: <i>Salimo 5:1-8</i> Vesi Yoloweza: <i>Salimo 5:2</i></p> <p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Pemphero ndi kuyankhula ndi kumvetsera kwa Mulungu. 2. Pemphero ndi lofunika kwambiri chifukwa Mulungu ndi wofunikanso kwambiri. 3. Nthawi zina mapemphero athu sayankhidwa ndipo pali zifukwa zake. 	<p>Ndime Yowerenga: <i>Luka 11:1-10; Mateyu 6:5-15</i> Vesi Yoloweza: <i>Luka 11:9</i></p> <p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Ife tikuyenera kuzindikira kuti pemphero ndi mwayi wathu waukulu. 2. Ife tikuyenera kupemphera nthawi zonse. 3. Ife sitikuyenera kuti anthu azitiyamikira pa nthawi ya pemphero.
MAWU OYAMBA	<ul style="list-style-type: none"> • Ganizani mavuto amene amakhalapo mukafuna kulumikizana ndi anzanu ndiponso abale anu amene ali kutali. • Lingalirani za kudabwitsa kwa kuyankhulana ndi Mulungu. • Funsani ophunzira ngati amapemphera. Chifukwa chiyani? Ngati si choncho ndi chifukwa chiyani? 	<ul style="list-style-type: none"> • Ganizani mavuto amene amakhalapo mukafuna kulumikizana ndi anzanu ndiponso abale anu amene ali kutali. • Lingalirani za kudabwitsa kwa kuyankhulana ndi Mulungu. • Ganizirani zimene tikuyenera kumapempherera. • Ganizirani ngati ophunzirawo mapemphero awo anayankhidwapo. Kodi iwo anachita chiyani pemphero lawo litayankhidwa?
KUTSIRIZA	<p>Perekani Nkhani ya m’Baibulo</p> <p>Kambiranani ndi Kufotokoza:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Ganizani kuti timayankhula ndi yani pamene tikupemphera ndipo muonenso mitu ina ya Masalimo amene Davide analemba. 2. Ganizani za nthawi imene Davide ankapemphera ndipo kambiranani nthawi imene ife tingapemphere. 3. Kuchokera pa Salimo lomwe tawerenga, kambiranani zomwe zimalepheretsa Mulungu kumva mapemphero athu. 4. Kuchokeranso pa Salimo limeneli pezani zomwe tikuphunzira zimene zingatithandize kukonzekera kuyankhula ndi Mulungu m’pemphero. 5. Davide anali ndi ubale wapadera ndi Ambuye. N’chifukwa iye akuti Mfumu yanga ndi Mulungu wanga pa vesi 2. Kodi ife tingakhale nawo motani ubale umenewu? 6. <i>Kambiranani ndi kufotokoza kufunika kwa pemphero. Mwachitsanzo: Kodi moyo wanu ungakhale wotani popanda pemphero.</i> 7. <i>Kodi tipempherere ziti?</i> <p>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze. Tsirizani Phunziro Loyamba.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera A – Pemphero ndi chiyani?</p>	<p>Perekani Nkhani ya m’Baibulo</p> <p>Kambiranani ndi Kufotokoza:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Nthawi ina Yesu ankapemphera ndipo ophunzira ake anamufunsa kuti awaphunzitse kupemphera. 2. Ganizirani za amene mukuyankhula naye nthawi ya pemphero ndipo kumbukirani dzina lomwe Yesu anagwiritsa ntchito. 3. Yesu anayamba pemphero lake ndi kuyamika Mulungu. <i>Kodi kuyamika Mulungu kutenge mbali yotani ya pemphero lathu?</i> 4. Ganizirani za mapempho ATATU amene Yesu anachita mu pemphero lake. 5. Werengani fanizo lomwe Yesu anayankhula pa (Luka 11:5-10) ndipo muganizire phunziro lalikulu lokhala ndi liwuma pa pemphero lomwe Yesu akuphunzitsa. 6. Ganizirani zomwe Yesu anaphunzitsa za pemphero pa Mateyu 6:5-15. 7. <i>Ganizirani chifukwa chomwe timapempherera kwambiri ngati zinthu sizikuyenda bwino.</i> 8. <i>Ndiponso ganizirani chifukwa chomwe pemphero limakhala lovuta nthawi zina.</i> <p>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze. Tsirizani Phunziro Loyamba.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera A – Kuphunzira za pemphero.</p>
KUKUMBUTSANA	<ol style="list-style-type: none"> 1. Kodi pali zinthu kapena anthu omwe akufunika pemphero lathu? 2. Kodi tipemphere kangati? Ndipo kwa nthawi yayitali bwanji? 3. Ganizirani za mapemphero a anthu ena m’Baibulo ndi zomwe tingaphunzire kuchokera pa mapemphero awo. 	<ol style="list-style-type: none"> 1. Yankhulani mwachidule zinthu ZISANU za pemphero zomwe zili m’Phunziro Loyamba ndipo funsani ophunzira akhale m’magulu kuti akambirane zoti apempherere zonse. 2. Lembani kalozera wa pemphero.
KHALANI MOYO UMENEWU	<p>Zomwe tikuphunzira m’phunziroli:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Kodi tikuyenera kuyankhula kwambiri kapena kumvetsera kwambiri pa nthawi ya pemphero? 2. Mwina tikuyenera kumva zomwe Mulungu akuyankhula tisanapemphere. 	<p>Zomwe tikuphunzira m’phunziroli:</p> <p>Ganizirani za nyengo zanu, zochitika m’banja, ku dera kwanu ndi dziko lonse zomwe mukuyenera kupempherera. Ganizirani zoyamika nthawi yanu ya pemphero chifukwa cha zomwe zayankhidwa.</p>

	<p>A8 – KALASI Lachitatu Phunziro Lachiwiri – Pemphero Mutu – Kodi Mulungu amamva mapemphero athu?</p>	<p>A8 – KALASI Lachinayi Phunziro Lachiwiri – Kukhala Mkhristu Mutu – Kuphunzira mawu a Mulungu</p>
	<p>Ndime Yowerenga: <i>Luka 18:9-14</i> Vesi Yoloweza: <i>Yakobo 4:6</i></p> <p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Sikofunika kupita ku tchalitchi kuti tipemphere kwa Mulungu: timapemphera malo ena aliwonse ndi nthawi iliyonse. 2. Mulungu akufuna kuti tidzichepetse ndi kukhala woona mtima popemphera. 	<p>Ndime Yowerenga: <i>Machitidwe 17:10-14; 2 Timoteyo 3:14-17</i> Vesi Yoloweza: <i>Salimo 119:105</i></p> <p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Kuwerenga Baibulo n'kofunika. 2. Ife tikuyenera kukhulupirira Baibulo chifukwa ndi Mawu a Mulungu.
<p>MAWU OYAMBA</p>	<ul style="list-style-type: none"> • Onaninso maphunziro onse a mu Phunziro Loyamba onena za pemphero. • Baibulo limati "Kunyada kumafikitsa ku chiwononengeko." (<i>Miyambo 16:18</i>) Kambiranani tanthauzo la mawu amenewa. • Perekani chitsanzo cha zomwe zinachitika kapena zopeka. 	<p>Dziwani kuti pa dziko lapansi pali Mabaibulo ambiri kuposa buku lina lililonse. Baibulo ndi buku lokhalo anthu ochulukana amagula. Zaka za m'mbuyumo anthu akhala akufuna kuononga Baibulo ndipo ena analiwochapo koma likanalipobe mpaka lero. Izi zili chomwewechi chifukwa ndi Mawu a Mulungu. (<i>Onani 1 Petulo 1 24-25.</i>)</p>
<p>KUTSIRIZA</p>	<p>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</p> <p>Kambiranani ndi Kufotokoza:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Yesu anaphunzitsa kuti tikuyenera kupemphera nthawi zonse ndi kuti tisafooke. (<i>18:1</i>) 2. Iye akufotokozanso kuti anthu amene ndi odzikweza ndi osadzichepetsa alibe zowayenera kupemphera. (<i>18:9</i>) 3. Taona kuchulukana kwa mawu akuti "Ine" kumene munthu wachipembezoyo (Mfarisi) wanena 4. Funsani ophunzira kuti afotokoze za pemphero ndi khalidwe la wolandira msonkho. 5. <i>Onani kusiyana kwa kapemphereredwe ka anthu awiriwa.</i> 6. <i>Onani za munthu amene anakondweretsa Mulungu mwa awiriwa ndi chifukwa chake.</i> <p>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze. Tsirizani Phunziro Lachiwiri.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera A – Kodi Mulungu amamva mapemphero athu?</p>	<p>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</p> <p>Kambiranani ndi Kufotokoza:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Kwa Mkhristu, Baibulo ndi chinthu chofunika kwambiri, koma tingadziwe bwanji kuti limanena zoonza? 2. Ndime Yowerenga ikutiwuzwa kuti Malemba anauziridwa ndi Mulungu, kutanthauza ndi mawudi a Mulungu. Mulungu sanganame, choncho ife timadziwa kuti Baibulo ndi loona. 3. M'Chipangano Chakale muli zambiri zomwe analosera ndipo zinachitika pa nthawi yake, mwinanso patapita zaka zambiri. Mwachitsanzo, ndime zonse za m'Chipangano Chakale zonena za kubadwa kwa Yesu. 4. Anthu pafupifupi makumi anayi ndi amene analemba Baibulo kwa zaka zambiri, koma muli nkhanu yayikulu imodzi ndi uthenga umodzi zimene zimasonyeza mgwirizano wa bukuli. 5. Fotokozani wachidule zomwe zinachitika ku Bereya, ndi kuonetsa momwe anthu a ku Bereya ankalemekezera Malemba. (<i>Machitidwe 17:10-12</i>) 6. Kuwerenga Baibulo ndi kutsatira ziphunzitsa zake kudzachititsa Mzimu Woyera kusintha miyoyo ya anthu. 7. Sitidabwa lero kuti Baibulo ndi buku lofunika kwambiri. Pezani zifukwa zomwe ife tikuyenera kumawerengera Baibulo. <p>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze. Tsirizani Phunziro Lachiwiri.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera A – Kuphunzira mawu a Mulungu.</p>
<p>KUKUMBUTSANA</p>	<p>Lembani pa pepala khalidwe la wolandira msonkho ndipo pa pepala lina lembani khalidwe la Mfarisi.</p>	<p>Kambiranani Vesi Yoloweza ndipo jambulani chithunzi cha kuwala kuchokera mlengalenga. Pansi pa chomwe mwajambulacho mulembe zinthu zimene mukufuna kuti Mulungu akuunikireni. Chitsanzo: chisankho chomwe mukufuna kuchita kapena thandizo lomwe mukulifuna pamene mwakhumudwa.</p>
<p>KHALANI MOYO UMENEWU</p>	<p>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Kodi mawu akuti "kudzichepetsa" akutanthauza chiyani ndipo ife tingakhale bwanji odzichepetsa? Perekani zitsanzo za momwe tingaonetsere kudzichepetsa kwathu. 2. Kodi mawu akuti "kunyada" akutanthauza chiyani ndi momwe ife tingakhaliwe osanyada? Perekani zitsanzo za momwe tingaonetsera kunyada kwathu. 	<p>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Kodi ndi ziti zomwe mungachite kuti kuwerenga Baibulo kukhale kosavuta kwa inu? 2. Kambiranani za kupemphera ndi kufunsa Mulungu kuti akuthandize kuwerenga Baibulo nthawi zonse, kumvetsetsa, ndi kugwiritsa ntchito pa moyo wanu.

	A8 – KALASI Lachitatu Phunziro Lachitatu – Pemphero Mutu – Kodi tingapemphere motani?	A8 – KALASI Lachinayi Phunziro Lachitatu – Kukhala Mkhristu Mutu – Kukhala moyo wokondweretsa Mulungu
	<p>Ndime Yowerenga: <i>Mateyu 6:5-15</i> Vesi Yoloweza: <i>Mateyu 6:8</i></p> <p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Tikuyenera kupemphera nthawi zonse osati pa nthawi yomwe zinthu sizikuyenda bwino kokha. 2. Mapemphero athu asachite kukhala okonzedwa bwino kapena aatali. 3. "Pemphero la Atate" ndi ndondomeko imene tikuyenera kutsatira pamene tikupemphera. 	<p>Ndime Yowerenga: <i>Yohane 15:1-17; Agalatiya 5:19-23</i> Vesi Yoloweza: <i>Yohane 15:5</i></p> <p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Akhristu akuyenera kukhala nthawi zonse ofanana ndi Yesu. 2. Chinsinsi chake ndi chokhala mwa lye monga akufotokoza mu fanizo la mpesa ndi nthambi zake. 3. Akhristu akuyenera kuyanjana ndi Mulungu kuti aziwasadza kuti abereka zipatso zochuluka.
MAWU OYAMBA	<ol style="list-style-type: none"> 1. Onaninso Phunziro Loyamba ndi 2 ndi zonse zomwe mwaphunzira za pemphero. 2. Pezani chifukwa chomwe pemphero ndi chinthu cha kukhala chinthu chovuta. 3. Kodi ubwino opemphera mokweza mawu ndi wotani? 4. Kodi ubwino wolembe mapemphero athu ndi wotani? 	<ol style="list-style-type: none"> 1. Kambiranani za mawu awa - "Timafanana ndi gulu lomwe timakhala nalo." (Mwana mbuu, make mbuu.) 2. Nthawi zambiri amati Baibulo ndi buku la chinthunzi. Zinthunzi zake zili m'mawu ake. Mu phunziro lino moyo wa Mkhristu uli ngati nthambi ya mtengo wa mpesa.
KUTSIRIZA	<p>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</p> <p>Kambiranani ndi Kufotokoza:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Ambuye anaphunzitsa za pemphero pa Chiphunzitsa cha pa Phiri. 2. Fotokozani chifukwa chomwe pemphero ndi chinthu cha pakati pa munthu ndi Mulungu basi. 3. Fotokozani kusafunika komabwereza mawu omwewo popemphera. 4. Kambiranani za kufunika kwa pemphero ngakhake kuti "Atate akudziwa kale zomwe tikuzifuna tisanapemphe." 5. Ganizirani za ndondomeko ya kapemphereredwe komwe kali mu Pemphero la Ambuye polingalira za Kuyamika ndi Kupempha. 6. Kambiranani za kufunika kwa kukhulupirira Mulungu pamene tikupemphera kuti zopempha zathu zichitike. <p>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze. Tsirizani Phunziro Lachitatu.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera A – Kodi tingapemphere motani?</p>	<p>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</p> <p>Kambiranani ndi Kufotokoza:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Fotokozani za Atate ngati mwini munda, Ambuye ngati mpesa, ndipo Akhristu ngati nthambi. 2. Fotokozani kuti Mulungu amafuna kuti tibereke zipatso m'moyo mwathu, ndipo izi azifotokoza bwino pa Agalatiya 5:22-23. 3. Takambiranani za mmene mitengo ya zipatso imaonekera asanayisadze komanso ndi kufunika kosadza mitengo imeneyi kuti ibale zipatso zochuluka. 4. Siyanitsani ndi Agalatiya 5:19-20 pamene pali zipatso za thupi la munthu lomwe Mzimu Woyera sakugwiramo ntchito yake ndipo sakhulupirira Khristu. 5. Kumbutsani ophunzira kuti cholinga cha Mulungu ndi chakuti Mkhristu aliyense akhale monga Khristu, amene anaonetsa chipatso chonse cha Mzimu m'moyo wake. <p>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze. Tsirizani Phunziro Lachitatu.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera A – Kukhala moyo wokondweretsa Mulungu.</p>
KUKUMBUTSANA	<ol style="list-style-type: none"> 1. Ganizirani zomwe zili pa 1 Timoteyo 2:1 ndipo kambiranani za mitundu ya pemphero. 2. Pezani malo amene mungakapemphere mwanseri. Lembani malo amene ophunzira akutchula. 	<ol style="list-style-type: none"> 1. Fotokozani za Akhristu amene amaonetsa chipatso chonse cha Mzimu m'moyo wawo ndipo muganizire za kupindula kumene kuli m'moyo wawo. 2. Fotokozani momwe Mulungu angagwirire ntchito m'miyoyo yathu kuti achotse zosafunika zonse, monga makhalidwe onse auchimo monga momwe mlimi amasadzira mpesa wake.
KHALANI MOYO UMENEWU	<p>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Pemphero si chinthu chopanda moyo koma ndi chamoyo. 2. Fotokozani kuti zimenezi zikutanthauza chiyani pamene mukupemphera. 3. Pemphani Mulungu kuti akupatseni chikhulupiriro pamene mukupemphera. 4. Gwiritsani ntchito ndondomeko yomwe ili mu Pemphero la Ambuye kuti ophunzira akhale ndi mapemphero awo. 	<p>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</p> <p>Pemphani ophunzira kuti awerenge mwapemphero Agalatiya 5:22-23, kupempha Mulungu kuti awasonyeze mtundu wa zipatso kapena makhalidwe amene akuyenera kukhala nawo.</p>

	<p>A8 – KALASI Lachitatu Phunziro Lachinayi – Pemphero Mutu – Kodi Mulungu amayankha pemphero?</p>	<p>A8 – KALASI Lachinayi Phunziro Lachinayi – Kukhala Mkhristu Mutu – Kupereka kwa Mulungu</p>
	<p>Ndime Yowerenga: 1 <i>Samuele 1:1-20</i> Vesi Yoloweza: 1 <i>Samuele 1:20</i></p> <p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ol style="list-style-type: none"> Hana anapemphera kuti Mulungu amupatse mwana. Mapemphero athu sayankhidwa m'njira imene ife tikufuna nthawi zonse, kapena mofulumira momwe tikanafunira. Mulungu amayankha ndipo zolinga zake ndi zabwino kuposa zolinga zathu. 	<p>Ndime Yowerenga: <i>Marko 12:41-44; Mateyu 6:1-4</i> Vesi Yoloweza: 2 <i>Akorinto 9:7</i></p> <p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ol style="list-style-type: none"> Ife tipereke kwa Mulungu mokondwera, monga udindo wofunika kwambiri pa moyo wathu wa Chikhristu. Zopereka kwa Mulungu si ndalama zokha.
<p>MAWU OYAMBA</p>	<p>Fotokozani nkhani ya Hana ndi mmene analili. Matani pepala pa khoma ndipo pakhale zithunzi ndi mawu owonetsa zomwe Hana anamva: ASANAPEMPHERE + ATAPEMPHERA</p>	<p>M'magulu ang'onoang'ono, khalani mozungulira ndipo mulembe zinthu zimene Mulungu amatipatsa, ndiponso zinthu zimene ife timapereka kwa Mulungu.</p>
<p>KUTSIRIZA</p>	<p>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</p> <p>Kambiranani ndi Kufotokoza:</p> <ol style="list-style-type: none"> Fotokozani mwachidule nkhani ya Hana ndi banja lake. Fotokozaninso za maulendo a ku Nyumba ya Mulungu kukapereka nsembe ndi kukapembedza chaka chilichonse. Fotokozani momwe Hana ankamvera mu mtima mwake chifukwa chopanda ana ndi zomwe ankamuchita Penina. Onani pemphero la Hana ndi lonjezo lomwe anachita kwa Ambuye. Fotokozani zomwe anachita wansembe Eli ataona Hana akupemphera. Fotokozani momwe Mulungu anayankhira pemphero la Hana. Taganizani anamva bwanji mu mtima mwake atatula nkhwana zake kwa Ambuye. <p>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze. Tsirizani Phunziro Lachinayi.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera A – Kodi Mulungu amayankha pemphero?</p>	<p>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</p> <p>Kambiranani ndi Kufotokoza:</p> <ol style="list-style-type: none"> Fotokozani zochitika m'Nyumba ya Mulungu pamene Yesu ankaona anthu akupereka. Fotokozani chifukwa chomwe chopereka cha mayi wamasiye chinali chosiyana ndi cha aliynse. N'chifukwa chiyani Yesu anakondwera ndi chopereka chochepa cha mayi ameneyu? Kodi nkhani imeneyi ikutiphunzitsa chiyani pa zakupereka nthawi yathu, maluso athu, kapena chuma chatu kwa Ambuye? Kodi n'chifukwa chiyani Mulungu amatilangiza kuti tizipereka mosadzionetsera? <i>Fotokozani lonjezo la Mulungu kwa amene amapereka mosadzionetsera.</i> <p>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze. Tsirizani Phunziro Lachinayi.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera A – Kupereka kwa Mulungu.</p>
<p>KUKUMBUTSANA</p>	<ol style="list-style-type: none"> Funsani ophunzira ngati tsiku lina anakhumudwa chifukwa cha zomwe zinawachitikira. Kambiranani zomwe ankayenera kuchita kuti athandizidwe nthawi imeneyo. Perekani kwa ophunzira kadi, ndipo awuzeni kuti alembe nkhwana zawo ndipo azipereka kwa Ambuye. 	<p>Pezani mavesi ena m'Baibulo amene akufotokoza za chopereka, chitsanzo: "Yesu anati, kupereka kumadalitsa kuposa kulandira." (Machitidwe 20:35) Pemphani Mulungu kuti akuthandizeni kumvetsa fundo imeneyi.</p>
<p>KHALANI MOYO UMENEWU</p>	<p>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</p> <ol style="list-style-type: none"> Ganizani za munthu wina amene angapindule atazindikira kuti Mulungu atha kusenza nkhwana zake kuti apeze mtendere. Kodi n'koyenera kupita kwa iwo msanga kuti akawuzidwe nkhani imeneyi? 	<p>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</p> <ol style="list-style-type: none"> Ganizirani njira zomwe mungamaperekere kwa Ambuye. Sankhani njira imodzi ndipo yambani kupereka chifukwa cha phunziro la leroli. Limbikitsani ophunzira kuti nthawi zonse azikhala ndi zolinga zabwino pamene akupereka.

	A9 – KALASI Lachitatu Phunziro Loyamba – Zochita za Paulo Mutu – ‘Wozunza Akhristu’	A9 – KALASI Lachinayi Phunziro Loyamba – Mtumwi Paulo Mutu – Kusinthika kwake
	<p>Ndime Yowerenga: <i>Machitidwe 9:1-19</i> Vesi Yoloweza: <i>2 Akorinto 5:17</i></p> <p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Saulo (Paulo) anasinthika atakumana ndi Khristu. 2. Mulungu akusinthabe miyoyo lero. 	<p>Ndime Yowerenga: <i>Machitidwe 9:1-30</i> Vesi Yoloweza: <i>2 Akorinto 5:17</i></p> <p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Saulo (Paulo) anasinthika atakumana ndi Khristu. 2. Ndi Mulungu yekha amene amasintha miyoyo. 3. Kukhala Mkhristu kutha kukhala kovuta, koma Mulungu amakhala ndi Akhristu mu nthawi yawo ya zovuta.
MAWU OYAMBA	<ul style="list-style-type: none"> • Fotokozani za Paulo monga mmodzi wa anthu ofunika kwambiri m'Chipangano Chatsopano. Fotokozani za kukhudzidwa kwake ndi imfa ya Stefano. (<i>Machitidwe 6:58</i>) • Gwiritsani chitsanzo cha mbozi imene imasintha ndi kukhala gulugufe pamene mukufotokoza za kusandulika kwa munthu. 	<ul style="list-style-type: none"> • Fotokozani za Paulo monga mmodzi wa anthu ofunika kwambiri m'Chipangano Chatsopano. Fotokozani za kukhudzidwa kwake ndi imfa ya Stefano. (<i>Machitidwe 6:58</i>) • Gwiritsani chitsanzo cha mbozi imene imasintha ndi kukhala gulugufe pamene mukufotokoza za kusandulika kwa munthu
KUTSIRIZA	<p>Perekani Nkhani ya m’Baibulo</p> <p>Kambiranani ndi Kufotokoza:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Fotokozani kuti Paulo ankadziwika kuti Saulo mpaka nthawi ina m’tsogolo. 2. Fotokozani chifukwa chomwe iye ankapitira ku Damasiko. 3. Fotokozani bwino zomwe zinachitika ndi zomwe Ambuye anayankhula atakumana ndi Saulo. Zomwe Paulo akufotokoza ndi zothandiza kwambiri kudziwa zomwe zinachitika. (<i>Machitidwe 22:1-13 ndi 26:9-18</i>) 4. Fotokozani zomwe zinachitika atapita naye ku Damasiko ndi ntchito imene anatumidwa. 5. <i>Pezani tanthauzo la mawu akuti “kusandulika.” Kusandulika ndi ntchito ya chisomo cha Mulungu yolenganso mwatsopano mwa Khristu. Izi zikufanana ndi kubadwa mwatsopano. (Yohane 3:3)</i> 6. Fotokozani momwe Paulo anasinthira atakumana ndi Khristu. 7. <i>Tsindikani kufunika kwa uthenga umenewu pa chikhulupiriro cha Chikhristu.</i> <p>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze. Tsirizani Phunziro Loyamba.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera A – ‘Wozunza Akhristu’.</p>	<p>Perekani Nkhani ya m’Baibulo</p> <p>Kambiranani ndi Kufotokoza:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Fotokozani kuti Paulo ankadziwika kuti Saulo mpaka nthawi ina m’tsogolo. 2. Fotokozani chifukwa chomwe iye ankapitira ku Damasiko. 3. Fotokozani bwino zomwe zinachitika ndi zomwe Ambuye anayankhula atakumana ndi Saulo. Zomwe Paulo akufotokoza ndi zothandiza kwambiri kudziwa zomwe zinachitika. (<i>Machitidwe 22:1-13 ndi 26:9-18</i>) 4. Fotokozani zomwe zinachitika atapita naye ku Damasiko ndi ntchito imene anatumidwa. 5. Kukhala Mkhristu si kophweka. Fotokozani zovuta zimene Saulo anakumana nazo masiku ake woyamba kutsatira Ambuye. 6. <i>Fotokozani kuti kusandulika ndi ntchito ya chisomo cha Mulungu yolenganso mwatsopano mwa Khristu. Izi zikufanana ndi kubadwa mwatsopano. (Yohane 3:3)</i> 7. Fotokozaninso kuti Saulo sanasanduke munthu “wachipembedzo” chifukwa iye anali kale wachipembedzo asanasandulike mtima. <p>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze. Tsirizani Phunziro Loyamba.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera A – Kusinthika kwake.</p>
KUKUMBUTSANA	<p>Khomani chipepala pa khoma chomwe mulembepo kuti: ‘Saulo – Asanasandulike ndi Atasandulika.’ Gwiritsani ntchito mbozi ndi gulugufe kuti zikuthandizeni kufotokoza bwino.</p>	<p>Mafunso kwa ophunzira:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Kambiranani zomwe zinasintha m’moyo wa Paulo atakhala Mkhristu. 2. Kodi iye anakumana ndi zovuta zotani? 3. Kodi miyoyo yathu imasintha motani pamene takhala Akhristu?
KHALANI MOYO UMENEWU	<p>Zomwe tikuphunzira m’phunziroli:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Limbikitsani ophunzira kuti aone za moyo wawo. 2. Kodi tikuphunzira chiyani pa nkhani ya kumvera kwa Ananiya? Lembani “zochita” zomwe taphunzira pa nkhani ya kumvera. 3. Pezani zomwe Akhristu angachite pofuna kulimbikitsa Akhristu atsopano. Lembani zimenezo ndipo muyike ndondomeko yotsatira zimenezo. 	<p>Zomwe tikuphunzira m’phunziroli:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Limbikitsani ophunzira kuti aone za moyo wawo. 2. Pemphererani Akhristu amene lero akuzunzika chifukwa cha chikhulupiriro chawo. 3. Werangani <i>1 Timoteyo 1:12-16</i>. Pitani mukagawe ndi ena zomwe zili pa vesi 15 amene si Akhristu.

	A9 – KALASI Lachitatu Phunziro Lachiwiri – Zochita za Paulo Mutu – ‘Masautso ake’	A9 – KALASI Lachinayi Phunziro Lachiwiri – Mtumwi Paulo Mutu – Maulendo ake
	<p>Ndime Yowerenga: <i>Machitidwe 9:19-30</i> Vesi Yoloweza: <i>Aroma 1:16</i></p> <p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ol style="list-style-type: none"> Masiku oyamba a moyo wa Chikhristu wa Saulo anali ovuta kwambiri Nthawi zina ndi kovuta kukhala Mkhristu chifukwa si aliyense amene amagwirizana nawo Uthenga Wabwino. N'kofunika kwambiri kulimbikitsa Akhristu atsopano. 	<p>Ndime Yowerenga: <i>Machitidwe 11:19-26; 13:1-12</i> Vesi Yoloweza: <i>Machitidwe 13:12</i></p> <p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ol style="list-style-type: none"> Masiku oyamba a moyo wa Chikhristu wa Saulo anali ovuta. Kusandulika ndi chiyambi cha moyo watsopano mwa Khristu. N'kofunika kuphunzitsa Akhristu atsopano kuti akule mu chidziwitso chawo cha moyo wa Chikhristu.
MAWU OYAMBA	<ul style="list-style-type: none"> Kambiranani za kufunika kwa kulimbikitsidwa. Funsani ophunzira kuti apereke chitsanzo cha nthawi imene analimbikitsidwa pa miyoyo yawo ndi kufunika kwake. 	<ul style="list-style-type: none"> Kambiranani za kufunika kwa chakudya ngati munthu akufuna kukula bwino. Fotokozani za kukula pa moyo wauzimu wa Chikhristu. Ngati muli ndi Mabaibulo, funsani wina kuti awerenge 1 Petulo 2:2 ndi 2 Petulo 3:18.
KUTSIRIZA	<p>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</p> <p>Kambiranani ndi Kufotokoza:</p> <ol style="list-style-type: none"> Fotokozani zomwe zinachitika pamene. Fotokozani chifukwa chomwe Ayuda ankadana naye ndiponso zomwe anachita kuti athawe. Kambiranani mavuto a Saulo ndiponso chifukwa chomwe anthu ankakanira Uthenga Wabwino. N'chifukwa chiyani Saulo sankachita manyazi ndi Uthenga Wabwino? (Onani Vesi Yoloweza.) Fotokozani mavuto amene anakumana nawo atabwerera ku Yerusalemu. Yankhulani za kufunika kwa Barnaba kwa Saulo ndiponso kufunika kwa chilimbikitsa m'moyo wa Mkhristu. Werengani 1 Samuele 30:6. <p>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze. Tsirizani Phunziro Lachiwiri.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera A – ‘Masautso ake’.</p>	<p>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</p> <p>Kambiranani ndi Kufotokoza:</p> <ol style="list-style-type: none"> Stefano ataphedwa, Akhristu anabalalikirira ku madera ambiri ndipo ena anapita ku Antiokeya. Iwo anafalitsa nkhanu yabwino ya Yesu ndipo ambiri anakhulupirira ndi kutembenukira kwa Ambuye. Barnaba anatimidwa mu Yerusalemu kupita kukathandiza Akhristu atsopano. Iye anazindikira kuti imeneyi inali ntchito yayikulu, choncho anapita kukafuna Saulo ku Antiokeya ndipo kwa chaka chathunthu anaphunzitsa mu mpingo kumene ndipo chiwerengero cha mpingo chinakula. Nthawi imeneyi, Mzimu Woyera anawuza mpingo kuti atumize Barnaba ndi Saulo ku madera atsopano. Iwo ananyamuka ulendo wopita ku Kupro kumene anakumana ndi chotchinga. Iwo anakumana ndi munthu wotchidwa Elimasi, munthu wamatsenga amene ankafuna kutchinga Sergio Paulosi kuti asakhale Mkhristu. Saulo anayankhula mwaulamuliro ndipo Elimasi anakhala ndi khungu ndipo Sergio Paulosi anakhulupirira Ambuye Yesu. <i>Tsindikani kufunika koyankhula mawu a Mulungu pochitira umboni. (Machitidwe 11:19-20)</i> <i>Tsindikani kufunika kwa kukula monga Akhristu. (1 Petulo 2:2)</i> <p>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze. Tsirizani Phunziro Lachiwiri.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera A – Maulendo ake.</p>
KUKUMBUTSANA	<p>Kambiranani zovuta za m'moyo wa Mkhristu pogwiritsa ntchito zomwe zinamuchitikira Saulo.</p>	<p>Mafunso kwa ophunzira: Kumbutsanani phunziroli pogwiritsa ntchito mafunso awa:</p> <ol style="list-style-type: none"> Kodi utumiki wa Saulo ndi Barnaba unali wopambana? Fotokozerani yankho lanu. Kodi tikuphunzira chiyani za mphamvu ya Mulungu pa mizimu yoyipa pamene Saulo anakumana ndi Elimasi?
KHALANI MOYO UMENEWU	<p>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</p> <ol style="list-style-type: none"> Nthawi zina anthu amaganiza kuti “Moyo wa Chikhristu ndi opanda mavuto.” Kodi mukuganiza kuti anthu amaganizo otere, Paulo akanawalangiza chiyani? Lingalirani 2 Akorinto 11:23-33. Lembani pemphero la chilimbikitsa kwa Akhristu amene akudutsa m'amasautso. Konzani kapepala koyika m'buku kokhala ndi pemphero ndipo perekani kwa Mkhristu amene akudutsa m'amasautso. 	<p>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</p> <ol style="list-style-type: none"> Funsani ophunzira kuti ayankhule za mlaliki wa Chikhristu amene akumudziwa ndipo afotokoze za kutembenuka mitima kwa anthu mu utumiki wake. Kodi zimenezi zikukutakasani motani inu? Kambiranani ndi mtsogoleri wa Chikhristu amene mukumudziwa kuti muthandizike pokhala ndi chidziwitso cha Baibulo ndikuti mukhale ndi machitidwe anu akawerengedwe ka Baibulo.

	A9 – KALASI Lachitatu Phunziro Lachitatu – Maulendo a Paulo Mutu – ‘Paulo mlaliki’	A9 – KALASI Lachinayi Phunziro Lachitatu – Mtumwi Paulo Mutu – Ulaliki wake
	<p>Ndime Yowerenga: <i>Machitidwe 13:1-12</i> Vesi Yoloweza: <i>Machitidwe 13:12</i></p> <p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Saulo (Paulo) tsopano wasanduka mlaliki ndi mtumwi. 2. Mzimu Woyera akugwira ntchito ndipo Uthenga wabwino ukulalikidwa ku malo atsopano. 3. Panali mphamvu za Satana zomwe zinkalimbana ndi Uthenga Wabwino. 	<p>Ndime Yowerenga: <i>Machitidwe 13:13-52</i> Vesi Yoloweza: <i>Machitidwe 13:49</i></p> <p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Saulo (Paulo) tsopano ndi mlaliki ndi mtumwi. 2. Uthenga wa Khristu maziko ake ali mu Chipangano Chakale ndipo imfa ya Khristu ndi kuuka kwake zinali monga mwa chikonzero cha Mulungu. 3. Kukhululukidwa kwa machimo kumapezeka mwa Khristu yekha.
MAWU OYAMBA	<ul style="list-style-type: none"> • Fotokozani kwa ophunzira za kutchinga Mulungu kumene Satana amachita. • Fufuzani zimenezi kuchokera m’Munda wa Edeni ndipo kambiranani za nkhani ya kugwa kwa munthu. • Fotokozani kuti Satana lero akugwirabe ntchito m’njira zosiyanasiyana pofuna kutchinga kulalikidwa kwa Uthenga Wabwino wa Ambuye Yesu. 	<ul style="list-style-type: none"> • Funsani ophunzira kuti aganizire kufunika kwa kukhulukira. Ganizani zomwe zimachitika tsiku ndi tsiku zoyenera kukhulukira ena. • Ganizirani za kufunika kokhulukidwa ndi Mulungu. Kambiranani za kupambana kwa Khristu mu uthenga wa Chikhristu onena za kukhulukidwa kwa machimo. • Pezani maganizo olakwika pa nkhani ya kukhulukira.
KUTSIRIZA	<p>Perekani Nkhani ya m’Baibulo</p> <p>Kambiranani ndi Kufotokoza:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Stefano ataphedwa, Akhristu anabalikira ku madera ambiri ndipo ena anapita ku Antiokeya. 2. Iwo anafalitsa nkhani yabwino ya Yesu ndipo anthu ambiri anakhulupirira Ambuye. 3. Mpingo ku Yerusalemu unatumiza Barnaba kuti akathandize Akhristu atsopano. Iye atazindikira kuti imeneyi inali ntchito yayikulu, choncho anabweretsa Saulo ku Antiokeya ndipo kwa chaka chonse anaphunzitsa anthu ambiri mu mpingo. 4. Nthawi imeneyi Mzimu Woyera anauza Mpingo kuti atumize Barnaba ndi Saulo kukagwira ntchito yatsopano. 5. Iwo ananyamuka ndi kupita ku Kupro koma kumeneko anatchingidwa ndi Elimasi, munthu wamatsenga amene ankafuna kulepheretsa Sergio Paulosi kuti akhale Mkhristu 6. Saulo anamudzudza ndipo Elimasi anachita khungu ndipo Sergio Paulosi anakhulupirira Ambuye Yesu. 7. <i>Kambiranani za kupezeka kwa ziwanda ndi za kugwidwa ndi ziwanda.</i> 8. <i>Kambiranani kufunika kwa Uthenga Wabwino nthawi imeneyo komanso lero.</i> 9. <i>Ganizirani chifukwa chomwe Mulungu analangira Elimasi.</i> <p>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze. Tsirizani Phunziro Lachitatu.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera A – ‘Paulo mlaliki’.</p>	<p>Perekani Nkhani ya m’Baibulo</p> <p>Kambiranani ndi Kufotokoza:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Paulo tsopano wafika ku Antiokeya (Pisidiya). 2. Mu uthenga wake woyamba, iye akufotokoza mwatsatanetsatane mbiri ya Ayuda, ndipo akutsiriza ndi za kubwera kwa Yesu, imfa yake ndi kuuka kwa akufa. Iye akutsiriza ndi mawu akuti “Dziwani kuti mwa Yesu chikhulukiro cha machimo chikulalikidwa.” (13:38) 3. Iye atalalikira uthenga woyamba mu sunagoge, anayitanidwa kuti abwerenso Sabata linalo. 4. Sabata lotsatira pafupifupi anthu a mzinda wonse anabwera kudzamva Paulo zomwe zinachititsa atsogoleri achipembedzo kuchita nsanje. 5. Paulo anati popeza akana Mawu a Mulungu, iye atembenukira kwa Amitundu monga momwe zili pa Yesaya 49:6. 6. <i>Fotokozani chifukwa chomwe atsogoleri a Chiyuda ankafunira kuti Khristu afe.</i> 7. <i>Ganizirani chifukwa chomwe Yesu anafera ndi momwe imfa ndi kuuka kwake chinali chikonzero cha Mulungu.</i> 8. <i>Ganizirani za kupambana kwa Khristu monga Mpulumutsi. (Onani vesi 38-39.)</i> <p>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze. Tsirizani Phunziro Lachitatu.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera A – Ulaliki wake.</p>
KUKUMBUTSANA	<p>Bwerezani phunziroli pofuna ophunzira kuti aonetse momwe Mulungu anagonjetsera Satana m’phunziro limeneli.</p>	<p>Perekani mafunso kwa ophunzira ngati njira yokumbutsana zomwe aphunzira lero.</p>
KHALANI MOYO UMENEWU	<p>Zomwe tikuphunzira m’phunziroli:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Siyanitsani momwe anachitira Elimasi ndi Sergio Paulo atamva Uthenga Wabwino. Limbikitsani ophunzira kuti avomereze Uthenga Wabwino. 2. Mafilimu ambiri lero amaonetsa za matsenga. Kodi n’koyenera kuti Mkhristu adzionera zimenezi? Kambiranani m’kalasi. 	<p>Zomwe tikuphunzira m’phunziroli:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Kodi kupambana kwa Khristu monga Mpulumutsi kuli ndi phunziro lotani pa chikhaliidwe chatu? 2. Werengani Aefeso 4:32 ndipo limbikitsani ophunzira za momwe mawu a Paulo a kukhulukira akutikhudzira lero!

	A9 – KALASI Lachitatu Phunziro Lachinayi – Maulendo a Paulo Mutu – ‘Mzinda wogawanikana’	A9 – KALASI Lachinayi Phunziro Lachinayi – Mtumwi Paulo Mutu – Masautso ake
	<p>Ndime Yowerenga: <i>Machitidwe 13:13-16; 42-52</i> Vesi Yoloweza: <i>Machitidwe 13:49</i></p> <p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Paulo akupitiriza maulendo ake okalalikira. 2. N’kofunika kumvetsera Mawu a Mulungu. 3. Uthenga wa Khristu ndi wa munthu aliyense ndipo umabweretsa chimwemwe kwa amene amaulandira. 	<p>Ndime Yowerenga: <i>Machitidwe 14:1-28</i> Vesi Yoloweza: <i>Marko 16:20</i></p> <p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Paulo akupitiriza maulendo ake okalalikira. 2. Uthenga wa Khristu ukugawanitsa anthu ndipo ena akuchita zoyipa kwambiri akamva uthengawu. 3. Kukhala wokhulupirika kwa Khristu ndi kofunika kwambiri monga waonetsera Paulo.
MAWU OYAMBA	<ul style="list-style-type: none"> • Funsani ophunzira kuti afotokoze chifukwa chomwe akuganizira kuti Baibulo ndi lofunika kwambiri. (Onani kuchuluka kwa malo amene alemba kuti Mawu a Ambuye mu Ndime Yowerenga m’phunziroli.) • Fotokozerani ophunzira kuti nkhani yayikulu m’Baibulo ndi ya uthenga wa Khristu umene ndi wa kwa anthu onse. Akumbutseni kuti Akhristu ndi anthu ochokera ku mitundu ndi zikhalidwe zosiyanasiyana. 	<ul style="list-style-type: none"> • Funsani ophunzira kuti afotokoze tanthauzo la “kukhulupirika.” • Funsani ophunzira kuti apereke zitsanzo za kukhulupirika kwa tsiku ndi tsiku. • Ganizirani kuti ndi chifukwa chiyani kukhulupirika ndi kofunika.
KUTSIRIZA	<p>Perekani Nkhani ya m’Baibulo</p> <p>Kambiranani ndi Kufotokoza:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Paulo tsopano wafika ku Antiokeya wina (Pisidiya), kumene atamaliza kulalikira uthenga wake woyamba mu sunagoge anapemphedwa kuti abwerenso Sabata linalo. 2. Sabata linalo anthu onse mu mzindamo anabwera kudzamva zomwe Paulo ankalalikira ndipo izi zinachititsa atsogoleri a Ayuda kuchita nsanje. 3. Paulo anati chifukwa cha kukana kwawo Mawu a Mulungu, tsopano iye adzapita kwa anthu Amitundu monga analembera pa Yesaya 49:6. 4. Tsindikani za anthu amene ankamvera ulaliki wa Paulo. (13:16, 42, 43 ndi 48) 5. Fotokozani chifukwa chomwe poyamba Uthenga Wabwino unalalikidwa kwa Ayuda. 6. Fotokozani momwe Mawu a Mulungu anafalikira. (13:49) <p>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze. Tsirizani Phunziro Lachinayi.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera A – ‘Mzinda wogawanikana’.</p>	<p>Perekani Nkhani ya m’Baibulo</p> <p>Kambiranani ndi Kufotokoza:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Pamene Paulo ndi Barnaba anafika ku Ikoniya, Ayuda ambiri ndi anthu Amitundu anakhulupirira, koma Ayuda ena anayambitsa ziwawa. 2. Mzinda unagawikana chifukwa cha Uthenga Wabwino ndipo ena anakonza chiwembu, motero Paulo ndi Barnaba anathawa ndi kupita ku Lustra. 3. Kumeneko Mulungu anagwiritsa ntchito Paulo kuchiritsa munthu wolumala ndipo zotsatira zake anthu akumeneko anaganiza kuti iwo anali milungu, ndi kuti ankayenera kupereka nsembe kwa iwo. 4. Paulo ndi Barnaba anauza anthuwo kuti iwo ankafuna kuwachotsa anthuwo ku moyo wopembedza mafano opanda moyo nd kuwapititsa kwa Mulungu amene amapereka moyo. Iwo anafotokoza zonse zimene Mulungu amatipatsa. (14:17) 5. Ayuda ena anabwera kuchokera ku Antiokeya ndi ku Ikoniya ndipo anakopa anthu kuti agende miyala Paulo ndipo anamukoka ndi kupita naye kunjira kwa mzindawo poganiza kuti wafa. Mwachisomo Paulo sanafe ndipo tsiku linalo anapita ku Derbe. Kumeneko anthu ambiri anakhala ophunzira. 6. Kenaka iwo anabwerera ku Lustra, Ikoniya ndi ku Antiokeya kumene analimbikitsa Akhristu, komatu kutero kunali kuyika moyo wawo pa chiopsezo. 7. <i>Tsindikani chomwe Mulungu ali. (14:15-17)</i> 8. <i>Ganizirani za kufunika kwa kupirira – Monga Paulo ndi Barnaba. Onetsetsani vesi 22.</i> <p>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze. Tsirizani Phunziro Lachinayi.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera A – Masautso ake.</p>
KUKUMBUTSANA	<p>Kumbutsanani phunziroli pofunsa ophunzira kuti aonetsera momwe Mulungu wagonjetsera Satana m’phunziroli.</p>	<ol style="list-style-type: none"> 1. Perekani mafunso kwa ophunzira ngati njira yowakumbutsira zomwe aphunzira. 2. Kodi cholinga cha “zizindikiro ndi zodabwitsa” pa vesi 3 ndi chiyani? 3. Kodi Paulo ndi Barnaba akuonetsa kukhulupirika kwawo kwambiri kwa Mulungu mu ndime imeneyi? Kodi Mulungu amayembekezera kuti tipereke miyoyo yathu chifukwa cha ntchito yake?
KHALANI MOYO UMENEWU	<p>Zomwe tikuphunzira m’phunziroli:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Onani zomwe anthu Amitundu anachita amava uthenga wa Khristu pa vesi 42 ndi 48. Kodi kuchokera pamenepa ife tikuphunzira chiyani za zomwe tingachite tikamva uthenga wa Khristu? 2. Phunzirani za ntchito ya wa mishonale amene anayesetsa kufalitsa uthenga wa Khristu kwa anthu azikhalidwe zina. 	<p>Zomwe tikuphunzira m’phunziroli:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Nanga tingakhale okhulupirika kwa Mulungu motani? 2. Konzani chinthu choti mumate pa khoma chokhala ndi uthenga wa momwe Khristu amatsutsira za mafano mu m’bado wathu uno.

	<p>A10 – KALASI Lachitatu Phunziro Loyamba – Zochitika pa Maulendo a Paulo Mutu – Kuzunzika chifukwa cha Ambuye</p>	<p>A10 – KALASI Lachinayi Phunziro Loyamba – Paulo Mutu – Paulo ku Filipi</p>
	<p>Ndime Yowerenga: <i>Machitidwe 14:1-21</i> Vesi Yoloweza: <i>1 Petulo 4:16</i></p> <p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Paulo ndi Barnaba akupitiriza maulendo awo okalalikira. 2. Nthawi zina Akhristu amazunzidwa chifukwa cha chikhulupiriro chawo koma sakuyenera “kutaya mtima” pamene zinthu zikuvuta. 3. Akhristu amakhulupirira Mulungu Wamoyo amene ndi Mlengi ndipo amatisamalira. 	<p>Ndime Yowerenga: <i>Machitidwe 16:9-40</i> Vesi Yoloweza: <i>Machitidwe 16:31</i></p> <p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Paulo ndi Barnaba akupitiriza maulendo awo okalalikira. 2. N'zofunika kumvetsera ndi kumvera malangizo a Mulungu. 3. Mulungu amatsekula mitima ya anthu ndiponso kuti chipulumutso ndi cha aliyense kudzera mwa Ambuye Yesu Khristu. 4. Akhristu amamvera Ambuye Yesu pamene akubatizidwa.
<p>MAWU OYAMBA</p>	<ul style="list-style-type: none"> • Fufuzani pamodzi ndi ophunzira kufunika kokhulupirira Mulungu kuti ndi Mlengi. • Tsindikani za udindo wathu pamaso pa Mulungu ndi za kufotokoza zomwe timachita kwa Iye. 	<ul style="list-style-type: none"> • Perekani funso la chifukwa chomwe tonse tikuyenera kufuna chipulumutso cha Mulungu. • Fotokozani za chipulumutso cha Mulungu ndi momwe ife tingapulumukire pamene takhulupirira Ambuye Yesu koma osati mwa ntchito zathu.
<p>KUTSIRIZA</p>	<p>Perekani Nkhani ya m’Baibulo</p> <p>Kambiranani ndi Kufotokoza:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Pamene Paulo ndi Barnaba anafika ku Ikoniya Ayuda ambiri ndi Amitundu anakhulupirira koma Ayuda ena anayambitsa ziwawa. 2. Mzinda unagawanikana chifukwa cha Uthenga Wabwino ndipo ena anakonza chiwembu chofuna kugenda miyala Paulo ndi Barnaba ndipo iwo anathawira ku Lustra. 3. Kumeneko, Mulungu anagwiritsa ntchito Paulo kuchiritsa munthu wolumala ndipo zotsatira zake anthu akumeneko anaganiza kuti iwo anali milungu, ndi kuti ankayenera kupereka nsembe kwa iwo. 4. Paulo ndi Barnaba anauza anthuwo kuti iwo ankafuna kuwachotsa anthuwo ku moyo wopembedza mafano opanda moyo ndi kuwapititsa kwa Mulungu amene amapereka moyo. 5. Ayuda ena anabwera kuchokera ku Antiokeya ndi ku Ikoniya ndipo anakopa anthu kuti agende miyala Paulo ndipo anamukoka ndi kupita naye kunja kwa mzindawo poganiza kuti wafa. 6. Mwachisomo Paulo sanafe ndipo tsiku linalo anapita ku Derbe. 7. <i>Tsindikani chomwe Mulungu ali. (14:15-17)</i> 8. <i>Kambiranani za kufunika kwa kupirira – Monga Paulo ndi Barnaba.</i> <p>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze. Tsirizani Phunziro Loyamba.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera B – Kuzunzika chifukwa cha Ambuye.</p>	<p>Perekani Nkhani ya m’Baibulo</p> <p>Kambiranani ndi Kufotokoza:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Paulo analangizidwa kuti asapite ku madera ena a ku Asiya, koma analandira masomphenya usiku wina omuza kuti apite ku Makedoniya (Ulaya). 2. Fotokozani zomwe zinachitika kuti Uthenga Wabwino upite ku Ulaya. (16:9) 3. Ku Filipi, Paulo anakumana ndi gulu la amayi akupemphera m’mbali mwa mtsinje, ndipo mmodzi mwa iwo anali Lidia. (16:14) 4. Fotokozani tanthauzo lakuti Mulungu anatsekula mtima wa Lidia. (16:14) 5. Paulo atalamula mzimu woyipa kuti utulukuke mwa mtsikana woombeza, iye pamodzi ndi Sila anakaponyedwa m’ndende. 6. Kunachitika chivomerezi ndipo maunyolo a m’ndende onse anaduka. Woyang’anira ndende ankafuna kudzipha koma Paulo anamutsimikizira kuti palibe ndi mmodzi yemwe amene anathawa. 7. Fotokozani momveka bwino za funso limene woyang’anira ndende anafunsa ndiponso yankho la Paulo. (Machitidwe 16:31) 8. <i>Tsindikani kufunika kwa Ambuye Yesu Khristu pa nkhani ya chipulumutso.</i> <p>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze. Tsirizani Phunziro Loyamba.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera B – Paulo ku Filipi.</p>
<p>KUKUMBUTSANA</p>	<ol style="list-style-type: none"> 1. Lumikizani Phunziro lathu ndi Eksodo 20:1-6. Thandizani ophunzira kuti amvetse kuti Mulungu Wamoyo alipodi. 2. Pangani posita yomwe mujambulepo mafano a lero omwe amatisyanitsa ndi Mulungu. 	<p>Kumbutsanani phunziroli pofunsa mafunso awa:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Fotokozani zomwe zinachitika woyang’anira ndende uja atatembenuka mtima. 2. Kodi ubatizo ukuyenera kuchitika motani ndipo chomuyenera munthu kuti abatizidwe ndi chiyani? (16:15, 31-33)
<p>KHALANI MOYO UMENEWU</p>	<p>Zomwe tikuphunzira m’phunziroli:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Taganizani za kuti tikuyenera kufotokoza zomwe timachita pamaso pa Mulungu ndi momwe ife tikuyenera kukhalira. Kodi zimenezi zikusintha motani makhalidwe athu ngati Akhristu? 2. Kodi pa 14:15 tikuphunzirapo chiyani za kupembedza anthu “otchuka”? 	<p>Zomwe tikuphunzira m’phunziroli:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Kumvetsa kuti chipulumutso timalandira mwachisomo cha Mulungu. 2. Kufunika kwa ubatizo wa wokhulupirira.

	A10 – KALASI Lachitatu Phunziro Lachiwiri – Zochitika pa Maulendo a Paulo Mutu – Bwenzi la muyaya	A10 – KALASI Lachinayi Phunziro Lachiwiri – Paulo Mutu – Paulo ku Tesalonika ndi Bereya
	<p>Ndime Yowerenga: <i>Machitidwe 16:1-3; 2 Timoteyo 1:1-5</i> Vesi Yoloweza: <i>2 Timoteyo 3:15</i></p> <p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Kuwerenga ndi kudziwa Malemba zimatipatsa nzeru zotitsogolera ku chipulumutso. 2. N'kofunika kukhala ndi abwenzi a Chikhristu ndi kumapemphererana. 	<p>Ndime Yowerenga: <i>Machitidwe 17:1-14</i> Vesi Yoloweza: <i>Machitidwe 17:11</i></p> <p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Paulo ndi Sila anapitiriza ulendo wawo kupita ku Tesalonika ndi ku Bereya. 2. Yesu ndi Khristu, amene Chipangano Chakale chinanena za lye, ndipo imfa yake ndi kuuka kwake zinali zoyenera. 3. N'kofunika kumafufuza m'Malemba kuti tidziwe chikhulupiriro cha Chikhristu kuti ndi chotani.
MAWU OYAMBA	<ul style="list-style-type: none"> • Kambiranani zomwe zimatichititsa miyoyo yathu kukhala yabwino kapena yoyipa. • Fufuzani pamodzi ndi ophunzira kufunika kwa chikhaliidwe cha Chikhristu pa miyoyo yathu. • Yankhulani za amene anakulimbikitsa pa chikhulupiriro cha Chikhristu ndi zomwe iwo anachitira zimenezi. 	<ul style="list-style-type: none"> • Funsani ophunzira kuti atchule anthu amene amawatenga kukhala ofunika ndi chifukwa chomwe amaganizira kuti iwo ndi ofunika. • Fotokozani kuti uthenga wa Chikhristu ndi wa munthu wapadera kwambiri. Ayitaneni kuti amve uthenga umene mukuwerega pa <i>Machitidwe 17:1-14</i>.
KUTSIRIZA	<p>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</p> <p>Kambiranani ndi Kufotokoza:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Fotokozani za banja la Timoteyo. 2. Fotokozani udindo wa agogo ndi amayi ake pa Tiimoteyo pa chikhulupiriro chake. 3. <i>Ganizirani za kufunika kolemekeza banja la Chikhristu.</i> 4. Fotokozani chifukwa chomwe Paulo anaona kuti kunali koyenera kuti Timoteyo achite mdulidwe. Kodi pamenepa tikuphunzirapo chiyani? 5. Timoteyo anayamba kuyenda ndi Paulo ndipo anali thandizo lalikulu kwa iye. 6. Onani mawu a Paulo kwa Timoteyo m'kalata yake. (<i>2 Timoteyo 1:3-5</i>) <p>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze. Tsirizani Phunziro Lachiwiri.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera B – Bwenzi la muyaya.</p>	<p>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</p> <p>Kambiranani ndi Kufotokoza:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Paulo anachoka ku Filipi ndi kupita ku Tesalonika kumene anakalalikira m'sunagoge. 2. <i>Fotokozani uthenga umene Paulo analalikira mu sunagoge ku Tesalonika. Fotokozaninso tanthauzo la mawu akuti "Khristu" kuti ndi Mpulumutsi Wodzozedwa wa Mulungu.</i> 3. <i>Ganizirani zotsatira za uthenga umenewu.</i> 4. <i>Kambiranani za mawu otsatirawa: "Akhala akusokoneza dziko lonse lapansi." (17:6)</i> 5. Paulo ndi Sila, nthawi imeneyinso, anachoka kumeneku usiku mofulumira kwambiri ndipo anapita ku Bereya. 6. Ayuda a ku Bereya anali osiyana ndi a ku Tesalonika ndipo ankawerenga Malemba tsiku ndi tsiku. (<i>17:11-12</i>) 7. Komabe kumeneku anatsutsidwanso ndipo Paulo anaperekezedwa kupita ku Atene. 8. Fananitsani kutsutsidwa kumene Paulo ndi Sila anakumana nako ndi kutsutsidwa kumene lero Akhristu amakumana nakonso pa chikhulupiriro chawo. <p>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze. Tsirizani Phunziro Lachiwiri.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera B – Paulo ku Tesalonika ndi Bereya.</p>
KUKUMBUTSANA	Phunzirani Vesi Yoloweza ndipo kambiranani ndi kalasi momwe vesiyi ikufotokozera zonse zomwe taphunzira lero.	Werengani <i>Yoswa 1:8</i> ndipo fananizani ndi Vesi Yoloweza (<i>Machitidwe 17:11</i>). Kodi zimenezi zikutiphunzitsa chiyani lero ife monga Akhristu?
KHALANI MOYO UMENEWU	<p>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Kumvetsa za kufunika kokhala ndi abwenzi a Chikhristu. 2. Kufuna kukhala ndi abwenzi a Chikhristu. 3. Kupempherera anzathu ndi abale athu kuti akhulupirire mwa Ambuye Yesu. 	<p>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Kufunika kowerenga Baibulo ndi kupanga fundo zathu molingana ndi Baibulo. (Onani Vesi Yoloweza) 2. Momwe kukhulupirira Yesu monga Mfumu kungasinthire miyoyo yathu.

	<p>A10 – KALASI Lachitatu Phunziro Lachitatu – Zochitika pa Maulendo a Paulo Mutu – Paulo m'ndende</p>	<p>A10 – KALASI Lachinayi Phunziro Lachitatu – Paulo Mutu – Paulo kwa Atene ndi ku Korinto</p>
	<p>Ndime Yowerenga: <i>Machitidwe 16:16-34</i> Vesi Yoloweza: <i>Machitidwe 16:31</i></p> <p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Zomuchitikira Paulo ku Filipi. 2. Chipulumutso ndi mwa Ambuye Yesu Khristu. 3. Iwo amene apulumutsidwa akuyenera kubatizidwa. 	<p>Ndime Yowerenga: <i>Machitidwe 17:15-34; 18:1-18</i> Vesi Yoloweza: <i>Machitidwe 17:30-31</i></p> <p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Paulo tsopano akupita ku Atene ndi Korinto. 2. Mulungu akulamula kuti anthu atembenuke mtima. 3. Mulungu adzaweruzza dziko lapansi.
<p>MAWU OYAMBA</p>	<ul style="list-style-type: none"> • Fotokozerani ophunzira za nkhani ya kulanditsidwa. • Gwiritsani ntchito nkhaniyo pafotokoza tanthauzo la mawu akuti: 'kupulumutsidwa', 'Mpulumutsi', ndi 'chipulumutso'. • Uzani ophunzira kuti afotokoze za chipulumutso chawo ngati akudziwa kuti anapulumutsidwa. 	<ul style="list-style-type: none"> • Funsani ophunzira tanthauzo la kutembenuka mtima. • Gwiritsani ntchito 1 Atesalonika 1:9 pofuna kupereka tanthauzo la kutembenuka mtima. • Onani za fundo ya kutembenukira kwa Mulungu monga Mpulumutsi ndi kuti izi zimachititsa kuti munthu asiye makhalidwe ake akale. • Pofuna kutsindika za kutembenuka mtima, mulimbikitse kuti anthu ayankhule za amene anasinthika ndi Uthenga Wabwino.
<p>KUTSIRIZA</p>	<p>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</p> <p>Kambiranani ndi Kufotokoza:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Fotokozani zomwe zinachitika kuti Uthenga Wabwino upite ku Ulaya. (16:9) 2. Ku Filipi anakumana ndi gulu la amayi akupemphera m'mbali mwa mtsinje. 3. Fotokozani tanthauza lakuti Mulungu anatsekula mtima wa Lidia. (16:14) 4. Pamene Paulo analamula mzimu woyipa kuti utuluke mwa mtsikana woombeza, iye pamodzi ndi Sila anakaponyedwa m'ndende. 5. Kunali chivomerezi ndipo maunyolo a onse a m'ndende anaduka. Woyang'anira ndende ankafuna kudzipha koma Paulo anamuza kuti panalibe amene anathawa. 6. Fotokozani momveka bwino funso limene woyang'anira ndende anafunsa ndi yankho la Paulo. (Machitidwe 16:31) 7. <i>Tsindikani za ulamuliro wa dzina la Yesu. (16:18)</i> 8. <i>Fotokozani kuti nthawi zina Akhristu amazunzidwa. (16:23)</i> <p>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze. Tsirizani Phunziro Lachitatu.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera B – Paulo m'ndende.</p>	<p>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</p> <p>Kambiranani ndi Kufotokoza:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Paulo wafika ku Atene ndipo akuyendayenda mu mzindamo pamene akudikira anzake kuti afike. Iye wakhumudwa chifukwa cha kuchuluka kwa mafano. 2. Paulo anyamba kulalikira Yesu pa msika ndi m'masunagoge. 3. Paulo anatengedwa kupita ku bwalo lina kumene anafunsiwa kuti afotokoze za chiphunzitsa chatsapanochi. 4. Paulo anyankhula za Mulungu amene ndi Mlengi wamkulu amene analenga dziko lonse, ndipo anyankhula kuti Mulungu ameneyu sali kutali ndi anthu. Iye anafotokozanso kuti Mulungu adzaweruzza dziko lapansi kudzera mwa munthu mmodzi amene anamusankha ndi kumuukitsa kwa akufa. 5. Pamene anamva za kuuka kwa akufa, ambiri mwa iwo anamuseka, koma ena anakhulupirira. Paulo sanachedwe kumeneko; anapita ku Korinto. 6. Kumeneko anakumana ndi Akula ndi Prisila amene anyamba kumuthandiza. Iye anakhala ku Korinto miyezi 18 ndipo anthu ambiri anakhulupirira. 7. Machitidwe 18:9 - Mulungu anamutsimikizira kuti adzamuteteza mu Korinto. 8. <i>Tsindikani zomwe Paulo akuphunzitsa za Mulungu mu vesi 24-31.</i> 9. <i>Ganizirani za mtundu wa chilango.</i> 10. <i>Fotokozani zomwe anthu anachita atamva uthenga wa Paulo ku Atene ndi ku Korinto.</i> <p>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze. Tsirizani Phunziro Lachitatu.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera B – Paulo kwa Atene ndi ku Korinto.</p>
<p>KUKUMBUTSANA</p>	<p>Pangani zinthu zomwe zikufotokoza nkhani ya Paulo ndi Sila ku Filipi.</p>	<p>Fananizani machitidwe a Paulo pamene ankalalikira ku Atene ndi pamene ankalalikira ku Korinto. Kodi panali kusiyana m'machitidwe ake? Chifukwa chiyani?</p>
<p>KHALANI MOYO UMENEWU</p>	<p>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Za kufunika kodziwa kuti chipulumutso cha munthu ndi kudzera mwa Ambuye Yesu Khristu. 2. Kulengeza pa gulu kuti ndiwe wa Yesu kudzera mu ubatizo. 	<p>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Za kufunika kwa kutembenuka mtima ndi kuti Mkhristu akuyenera kumachoka ku machimo ake ndi kupita kwa Mulungu tsiku ndi tsiku. 2. Za kufotokozerana ena za Uthenga Wabwino ndi momwe Mulungu adzaweruzire dziko lapansi tsiku lina.

	<p>A10 – KALASI Lachitatu Phunziro Lachinayi – Zochitika pa Maulendo a Paulo Mutu – Mzinda wa Atene</p>	<p>A10 – KALASI Lachinayi Phunziro Lachinayi – Paulo Mutu – Paulo ku Efeso</p>
	<p>Ndime Yowerenga: <i>Machitidwe 17:10-34</i> Vesi Yoloweza: <i>Machitidwe 17:30</i></p> <p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Paulo akupita ku Atene. 2. Mulungu ndi Mulungu Wamoyo amene analenga dziko lapansi. 3. Mulungu akulamula anthu onse kuti atembenuke mtima. 4. Mulungu adzaweruzza dziko lapansi mwachilungamo. 	<p>Ndime Yowerenga: <i>Machitidwe 19:1-41</i> Vesi Yoloweza: <i>Aefeso 2:8-9</i></p> <p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Paulo akupita ku Efeso. 2. Mawu a Mulungu ndi ntchito ya Mulungu zinafalikira ku Efeso. 3. Dzina la Ambuye Yesu linakwezedwa kwambiri.
<p>MAWU OYAMBA</p>	<ul style="list-style-type: none"> • Funsani kalasi kuti akuuzeni zomwe amadziwa za mafano. • Afunseni akuuzeni tanthauzo la fano. • Kambiranani za malamulo awiri oyamba a pa <i>Eksodo 20</i>. • Gwiritsani ntchito <i>1 Atesalonika 1:9</i> pofotokoza tanthauzo la kutembenuka kuchoka ku mafano. 	<ul style="list-style-type: none"> • Kumbutsanani zomwe mwaphunzira mu Phunziro Lachitatu. • Ganizirani za kutembenuka mtima ndi zomwe zimachitika pa moyo wathu wa tsiku ndi tsiku. • Khalani ndi maganizo akuti kutembenuka mtima kumabweretsa kusintha pa moyo wathu. Kambiranani <i>Machitidwe 19:18-20</i>.
<p>KUTSIRIZA</p>	<p>Perekani Nkhani ya m’Baibulo</p> <p>Kambiranani ndi Kufotokoza:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Paulo wafika ku Atene ndipo akuyendayenda mu mzindamo pamene akudikira anzake kuti afike. Iye wakhumudwa chifukwa cha kuchuluka kwa mafano. 2. Paulo anayamba kulalikira Yesu pa msika ndi m’masunagoge. 3. Paulo anatengedwa kupita ku bwalo lina kumene anafunsidwa kuti afotokoze za chiphunzitsa chatsopanochi. 4. Paulo anayankhula za Mulungu amene ndi Mlenzi wamkulu amene analenga dziko lonse, ndipo anayankhula kuti Mulungu ameneyu sali kutali ndi anthu. Iye anafotokozanso kuti Mulungu adzaweruzza dziko lapansi kudzera mwa munthu mmodzi amene anamusankha ndi kumuukitsa kwa akuka. 5. Pamene anamva za kuuka kwa akufa, ambiri mwa iwo anamuseka, koma ena anakhulupirira. Paulo sanachedwe kumeneko; anapita ku Korinto. 6. <i>Tsindikani zomwe Paulo akuphunzitsa za Mulungu mu vesi 24-31.</i> 7. <i>Tsindikani kufunika kwa kuuka kwa akufa kwa Yesu. (17:31)</i> 8. <i>Kambiranani zomwe anthu anachita atamva ulaliki wa Paulo. (17:32-34)</i> <p>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze. Tsirizani Phunziro Lachinayi.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera B – Mzinda wa Atene.</p>	<p>Perekani Nkhani ya m’Baibulo</p> <p>Kambiranani ndi Kufotokoza:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Paulo tsopano akufika ku Efeso kumene wapeza ophunzira ena amene sanalandire Mzimu Woyera. 2. Fotokozani kufunika koti Paulo abatize ophunzira a Yohane. 3. Ayuda a mu sunagoge atakana uthenga wa Paulo; iye anakapeza malo ake kumene analalikira kwa zaka ziwiri. 4. Mulungu anachita zodabwitsa zambiri kudzera mwa Paulo. <i>(19:11)</i> Chifukwa cha mphamvu za Mzimu Woyera zomwe Paulo ankaonetsa, anthu ambiri anakhulupirira ndipo analengeza poyera za chikhulupiro chawo. Fotokozani zomwe iwo anachita. 5. Fotokozani mwachidule zomwe zinachititsa kuti kukhale ziwawa ku Efeso. <i>(19:23-41)</i> 6. <i>Fotokozani tanthauzo la mawu akuti ‘Ufumu wa Mulungu’. (19:8)</i> 7. <i>Fotokozanani momwe Mawu a Mulungu anapambanira ku Efeso. (19:20)</i> 8. <i>Kambiranani zomwe Akhristu atsopano akuyenera kuchita kuti athetsa makhali awo akale ndi zizolowezi zawo.</i> <p>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze. Tsirizani Phunziro Lachinayi.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera B – Paulo ku Aefeso.</p>
<p>KUKUMBUTSANA</p>	<ol style="list-style-type: none"> 1. Kambiranani m’magulu momwe mungatulire uthenga wa Chikhristu mokopa anthu m’dera lanu. 2. Konzani msonkhano wa momwe mungalalikire uthenga. 	<p>Lembani nkhani yoti muyike mu nyuzi ya zomwe zinachitika mu Machitidwe 19.</p>
<p>KHALANI MOYO UMENEWU</p>	<p>Zomwe tikuphunzira m’phunziroli:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Za kutembenuka mtima kwa munthu. Kodi zikutanthauza chiyani kuchoka ku tchimo? 2. Za kufunika kwa kulalikira. Kodi ife tingagawane bwanji ndi ena Uthenga Wabwino? 	<p>Zomwe tikuphunzira m’phunziroli:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Chikhulupiro cha Chikhristu chimadziwikinso kuti “Njirayo”. <i>(19:9)</i> Kodi zikutathauza chiyani? Kodi zimenezi zikutilimbikitsa motani? 2. Kodi ndi ziti zomwe tikuphunzira kuchokera pa zomwe anachita mlembi wa mzindawu <i>vesi 35-41?</i>

	A11 – KALASI Lachitatu Phunziro Loyamba – Zochitika pa Maulendo a Paulo Mutu – ‘Kugawana ndi anthu ena’	A11 – KALASI Lachinayi Phunziro Loyamba – Paulo m’Bwalo la Milandu Mutu – Yersualemu ndi gulu la anthu
	<p>Ndime Yowerenga: <i>Machitidwe 18:1-11</i> Vesi Yoloweza: <i>Machitidwe 18:9-10</i></p> <p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Paulo apita ku Korinto. 2. Uthenga wa Paulo kulikonse ankapita unali wakuti Yesu ndi Khristu. 3. Mulungu anali ndi Paulo ndipo anamulimbikitsa m’masomphenya. 	<p>Ndime Yowerenga: <i>Machitidwe 21:17-40; 22:1-30</i> Vesi Yoloweza: <i>Machitidwe 22:14-15</i></p> <p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Paulo atagwidwa mu Nyumba ya Mulungu anapereka umboni wake ku gulu la anthu. 2. Ayuda anayipidwa chifukwa chakuti anthu Amitundu analandira ndi kuvomereza Uthenga Wabwino. 3. Paulo anayankhula kwa nzika za Roma pamene ankafuna kumukwapula.
MAWU OYAMBA	<ul style="list-style-type: none"> • Fotokozerani ophunzira nkhani yanu ya momwe Mulungu anakulimbikitsirani. • Kambiranani tanthauzo ndi kufunika kwa chilimbikitso pa moyo wa Chikhristu. • Funsani ophunzira kuti apereke zitsanzo za chilimbikitso chomwe analandira. 	<ul style="list-style-type: none"> • Mwachidule fotokozani masautso umene Paulo anakumana nawo pamene anafika mu Yersualemu. • Pogwiritsa ntchito Voice of the Martyrs website (kapena njira ina), perekani zitsanzo za Akhristu amene anachitira umboni Yesu ndipo sanaope masautso. • Funsani ophunzira chifukwa chomwe Mkhristu angachitire zimenezi.
KUTSIRIZA	<p>Perekani Nkhani ya m’Baibulo</p> <p>Kambiranani ndi Kufotokoza:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Paulo wafika ku Korinto, ndipo wakumana ndi Akula ndi Prisilla amene ayamba kumuthandiza. 2. Mwachizolowezi tsiku la Sabata lililonse Paulo akupita ku sunagoge kukawuza Ayuda kuti Yesu ndi Mesiya amene akhala akumuyembekezera. 3. Pamene Ayuda ayamba kumunyoza, iye akupita ku nyumba ina ndi kuyamba kulalikira kwa anthu Amitundu. Anthu ambiri anakhulupirira ndipo anabatizidwa. 4. 18:9 - Mulungu anamutsimikizira kuti adzakhala ndi Paulo ku Korinto ndi kumuteteza. Fotokozani za chilimbikitso chachikulu chimenechi kwa Paulo. 5. <i>Tsindikani zomwe Paulo anachita kuti uthenga ufalikire. (18:4, 11)</i> 6. <i>Kambiranani momwe Mawu a Mulungu anafalikira ku Korinto ndiponso za kufunika kwa ubatizo.</i> <p>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze. Tsirizani Phunziro Loyamba.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera B – ‘Kugawana ndi anthu ena’.</p>	<p>Perekani Nkhani ya m’Baibulo</p> <p>Kambiranani ndi Kufotokoza:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Paulo wafika ku Yersualemu ndipo wapita ku Nyumba ya Mulungu. Iye anadzudzulidwa molakwika kuti anatenga wa Amitundu ndi kulowa naye m’Nyumbayo ndipo kunali chiwawa. 2. Iye anapulumutsidwa ndi mtsogoleri wa ankhondo wa Chiroma ndipo anamulola kuti ayankhule kwa gulu la anthu atayima pa masitepi a malo a asilikali. 3. Paulo anapereka umboni womveka bwino kwambiri. (22:1-21) Pamene anatchula kuti anatumidwa kuti apite kwa anthu Amitundu, anthu anayambanso za chiwawa zija. 4. Iye anatengedwa ndi kulowa naye kumalo a asilikali ndipo akanamukwapula ngati akanapanda kunena kuti iye ndi nzika ya Roma ndipo sakuyenera kukwapulidwa ngati sanaweruzidwe kuti ndi wolakwa. 5. <i>Tsindikani chifukwa chomwe Paulo anapitira ku Nyumba ya Mulungu.</i> 6. <i>Komanso tsindikani za kutembenuka mtima kwa Paulo.</i> 7. <i>Fotokozani chifukwa chomwe chinachititsa anthuwo kuti adane ndi Paulo.</i> <p>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze. Tsirizani Phunziro Loyamba.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera B – Yersualemu ndi gulu la anthu.</p>
KUKUMBUTSANA	Kumbutsanani nkhaninyi pofunsa mafunso.	Uzani kalasi kuti ikambirane ngati chinali chanzeru kuti Paulo apite ku Nyumba ya Mulungu pamene anafika mu Yersualemu.
KHALANI MOYO UMENEWU	<p>Zomwe tikuphunzira m’phunziroli:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Werengani Salimo 23 ndipo ganizirani za lonjezo la kupezeka kwa Mulungu momwe limatilimbikitsira ife monga Akhristu. 2. Kambiranani zomwe mungachite pofuna kulimbikitsa anthu ena pokhala nawo pamodzi. 	<p>Zomwe tikuphunzira m’phunziroli:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Akhristu akumangidwa tsiku ndi tsiku pa dziko lonse lapansi. 2. Khazikitsani nthawi ya mapempehero, kupempherera Akhristu amene akuzunzidwa. 3. Funsani ophunzira kuti alingalire za sabata yapita ndipo aone ngati anataya mwayi umene akanatha kuchitira umboni Khristu. 4. Afunseni kuti apemphe Mulungu kuti awathandize ndi kuwapatsa kulimba mtima pamene adzakhala akuchitira umboni nthawi ina m’tsogolo. 5. Funsani ophunzira akonze umboni wawo.

	<p>A11 – KALASI Lachitatu Phunziro Lachiwiri – Zochitika pa Maulendo a Paulo Mutu – ‘Chiwembu chofuna kumupha’</p>	<p>A11 – KALASI Lachinayi Phunziro Lachiwiri – Paulo m’Bwalo la Milandu Mutu – Ku Kaisareya ndi abwanamkubwa</p>
	<p>Ndime Yowerenga: <i>Machitidwe 23:10-24 ndi 24:22-27</i> Vesi Yoloweza: <i>Salimo 18:30</i></p> <p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Paulo tsopano wafika mu Yerusalemu. 2. Mulungu analimbikitsa Paulo pamene Ayuda ankafuna kumupha. 3. Paulo anapitiriza kulalikira Mawu a Mulungu mokhulupirika ngakhale anali wa m’ndende. 	<p>Ndime Yowerenga: <i>Machitidwe 23:23-26; 24:1-27; 25:1-12</i> Vesi Yoloweza: <i>1 Petulo 3:15</i></p> <p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Paulo anatengedwa kupita ku Kaisareya kuti atetezedwe ndipo kenaka anapempha kuti akuonekere pamaso pa Kaisara. 2. Pa milandu yake yambiri, Paulo ankalalikira za chilungamo, kudziletsa ndi chiweruzo chimene chikubwera. (24:25)
<p>MAWU OYAMBA</p>	<ul style="list-style-type: none"> • Kumbutsani ophunzira za mphamvu ya Ufumu wa Chiroma mu nthawi ya Paulo. • Fotokozani maonekedwe a chishango. Onetsani chithunzi cha msilikali wa Chiroma wa nthawi imeneyo atanyamula chishango. • Fotokozani momwe Yehova ndiye chishango cha anthu ake. Limbikitsani ophunzira kuti adziwe bwino Vesi Yoloweza – <i>Salimo 18:30</i>. 	<ul style="list-style-type: none"> • Lumikizani ndi nkhani ya Martin Luther zomwe anayankhula za Khristu pa mulandu wake ku Imperial Diet of Worms m’chaka cha 1521. • Ganizirani mawu amene Martin anayankhula ku Worms: "Pokhapokha Malemba atanditsimikizira momveka bwino...chikumbumtima changa ndi kapolo wa Mawu a Mulungu. Ine sindingachite kupena kusintha chilichonse, chifukwa kutsutsana ndi chikumbumtima changa sichinthu chabwino kapena cholondola. Mulungu thandizeni. Amenii." • Gwiritsani ntchito mawu amenewa ngati poyambira kufotokoza zomwe zinachitikira Paulo.
<p>KUTSIRIZA</p>	<p>Perekani Nkhani ya m’Baibulo</p> <p>Kambiranani ndi Kufotokoza:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Paulo ali pamaso pa Gulu Lolamulira la chipembedzo la Ayuda (Sanhedrin). 2. Panali chisokonezo chachikulu chifukwa Paulo anayankhula za kuuka kwa akufa, ena anakhulupirira koma ena ayi, choncho panabuka phokoso lalikulu. (23:9) 3. Moyo wa Paulo unali pa chiopsezo, choncho mkulu wolamulira ankhondo a Chiroma anabwera kudzamulanditsa. 4. Usiku umenewu Ambuye anaonekera kwa Paulo ndipo anamuuzza kuti alimbe mtima chifukwa apita ku Roma kumene akalalikira Uthenga Wabwino. 5. Ayuda ena anachita lumiro loti sadya kapena kumwa madzi mpaka Paulo atafa ndipo anakonza chiwembu chofuna kumupha. 6. Mwamwayi, mdzuku wa Paulo anamva za chiwembucho, ndipo anapita kukauza mkulu wa asilikali uja ndipo iye analamula kuti Paulo atetezedwe ndi kupita naye ku Kaisareya. 7. Kenaka Paulo anaonekera pamaso pa bwanamkubwa wa Chiroma, Felike, ndipo anafotokozanso Uthenga Wabwino. 8. <i>Tsindikani uthenga umene Paulo analalikira pamaso pa Felike ndi kufunika kwake lero.</i> <p>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze. Tsirizani Phunziro Lachiwiri.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera B – ‘Chiwembu chofuna kumupha’.</p>	<p>Perekani Nkhani ya m’Baibulo</p> <p>Kambiranani ndi Kufotokoza:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Paulo watengedwa kupita ku Kaisareya kuti atetezedwe ndipo akuonekera pamaso pa bwanamkubwa, Felike. 2. Kenaka akuzengedwa mlandu pamaso pa Felike pamene atsogoleri Achiyuda ananena kuti iye anadetsa Nyumba ya Mulungu ndiponso anayambitsa chiwawa. 3. Paulo anawayankha amene ankamunenawo, ndipo Felike analinsu ndi nthawi yake yomufunsa pamene iye anafotokoza momveka bwino chikhulupiro mwa Yesu Khristu. (24:24) 4. Paulo anakhala m’ndende zaka ziwiri mpaka pemene panabwera bwanamkubwa wina. 5. Tsopano Paulo akuonekera pamaso pa Festo ndipo atsogoleri Achiyuda abweranso kudzanena mulandu wawo. Paulo wakana kupita ku Yerusalemu ndipo wapempha kuti akaonekera pamaso pa Kaisara ndipo Festo walamula kuti iye apite ku Roma. 6. <i>Kambiranani momwe Paulo akudzitetezera pamaso pa Felike.</i> 7. <i>Ganizirani chifukwa chomwe chinachititsa kuti Felike anjenjemere pamene Paulo ankalalikira. (24:25)</i> 8. <i>Ganizirani chifukwa chomwe chinachititsa Paulo kupempha kuti akaonekere pamaso pa Kaisara ndi tanthauzo lake.</i> <p>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze. Tsirizani Phunziro Lachiwiri.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera B – Ku Kaisareya ndi abwanamkubwa.</p>
<p>KUKUMBUTSANA</p>	<p>Lembani zochitika za Paulo mutu wake ukhale: “Kuyembekezera malonjezo a Mulungu”.</p>	<p>Pangani chinthu chimene mulembepo kuti “Paulo atsimikiza kukhala mbali ya Yesu”.</p>
<p>KHALANI MOYO UMENEWU</p>	<p>Zomwe tikuphunzira m’phunziroli:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Ganizirani za lonjezo la Mulungu kwa Paulo usiku uja. Kodi chilipo kapena alipo amene akanalepheretsa lonjezo limeneli? Kodi zimenezi zikutilimbikitsa bwanji ife lero? 2. Felike ananjenjemera ndipo anachita mantha pamene anamva Mawu a Mulungu. (Machitidwe 24:25) Kodi ife timanjenjemera tikamva Mawu a Mulungu? 	<p>Zomwe tikuphunzira m’phunziroli:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Werengani ndipo lingalirani pa 2 Timoteyo 2:3. 2. Lembani zowawa zomwe tapirira nazo monga Akhristu. Kuonjezera pa zomwe tadutsamo, onaniso za chilimbikitso cha Mulungu mu nthawi zovutazi. 3. Paulo anagwiritsa ntchito unzika wake wa Chiroma pofalitsa Uthenga Wabwino. Kodi ife tingagwiritse motani mwayi umene tili nawo pofuna kufalitsa Uthenga Wabwino?

	A11 – KALASI Lachitatu Phunziro Lachitatu – Zochitika pa Maulendo a Paulo Mutu – ‘Paulo pamaso pa mfumu’	A11 – KALASI Lachinayi Phunziro Lachitatu – Paulo m’Bwalo la Milandu Mutu – Ku Kaisareya ndi mfumu
	<p>Ndime Yowerenga: <i>Machitidwe 25:13-22; 26:13-32</i> Vesi Yoloweza: <i>Machitidwe 26:22</i></p> <p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Tsopano Paulo akuyenera kudziteza yekha pamaso pa Festo. 2. Mfumu Agripa anakopedwa mpaka pofika kufuna kukhala Mkhristu. 	<p>Ndime Yowerenga: <i>Machitidwe 25:13-27; 26:1-32</i> Vesi Yoloweza: <i>Machitidwe 26:28</i></p> <p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Mulungu akulowerera pa moyo wa Paulo. Festo akuona kuti Paulo si woyenera kuphedwa, pamene Agripa akuona kuti Paulo akuyenera kumasulidwa. 2. Paulo akulengeza Uthenga Wabwino momveka bwino ndipo akufunitsitsa kukopa Agripa kuti akhale Mkhristu.
MAWU OYAMBA	<ul style="list-style-type: none"> • Funsani ophunzira zomwe akuganiza za zomwe munthu angakhaliye Mkhristu. • Fotokozani kuti anthu sakhala Akhristu mokakamidwa. • Kambiranani kufunika kokopa anthu kuti akhale Akhristu. • Kuchokera pa zomwe inu mukudziwa, perekani zitsanzo za kukakamidwa kwa anthu kuchita zinthu zomwe sakufuna kutero. 	<ul style="list-style-type: none"> • Yankhulani za udani umene tingakumane nawo pa chikhulupiro chathu cha Chikhristu. • Kodi ophunzira angachite chiyani nthawi ya udani umenewu? • Ganizirani za malonjezo amene Khristu anachita kwa ophunzira ake pa Luka 21:12-15. Onani momwe izi zingachitikire m’phunziro lino.
KUTSIRIZA	<p>Perekani Nkhani ya m’Baibulo</p> <p>Kambiranani ndi Kufotokoza:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Paulo wakhala m’ndende zaka ziwiri. Tsopano kwabwera bwanamkubwa watsopano, Festo. Ayuda akufuna kuti apite naye Paulo ku Yerusalemu kuti akazengedwe mlandu, koma Paulo akuti akufuna kupita ku Roma. 2. Mfumu Agripa ndi mkazi wake Benisi afika ku Kaisareya ndipo akufuna kumva za wam’ndende Paulo. 3. Abwera ndi Paulo pamaso pa Agripa. 4. Paulo akufotokoza mbiri ya moyo wake. (26:1-23) 5. Festo akuti Paulo ndi wamisala! Agripa akuvomereza kuti anatsala pang’ono kukhala Mkhristu. Onse anagwirizana kuti akanatha kumasula Paulo koma chifukwa wapempha kuti apite kwa Kaisara, anayenera kupita ku Roma. 6. Tsindikani za kudziteza kwa Paulo pamaso pa Festo ndi zomwe anagamula. (26:24-25) Ganizirani momwe Paulo anachitira kuti akope Agripa kuti akhale Mkhristu. 7. Ganizani za zomwe Paulo anayankha pa mawu a Agripa. (26:29) <p>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze. Tsirizani Phunziro Lachitatu.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera B – ‘Paulo pamaso pa mfumu’.</p>	<p>Perekani Nkhani ya m’Baibulo</p> <p>Kambiranani ndi Kufotokoza:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Paulo wakhala m’ndende zaka ziwiri. Tsopano kwabwera bwanamkubwa watsopano, Festo. Ayuda akufuna kuti apite naye Paulo ku Yerusalemu kuti akazengedwe mlandu, koma Paulo akuti akufuna kupita ku Roma. 2. Mfumu Agripa ndi mkazi wake Benisi afika ku Kaisareya ndipo akufuna kumva za wam’ndende Paulo. Abwera ndi Paulo pamaso pa Agripa. 3. Paulo akufotokoza mbiri ya moyo wake. (26:1-23) 4. Festo akuti Paulo ndi wamisala! Agripa akuvomereza kuti anatsala pang’ono kukhala Mkhristu. Onse anagwirizana kuti akanatha kumasula Paulo koma chifukwa anapempha kuti apite kwa Kaisara, anayenera kupita ku Roma 5. <i>Tsindikani za kudziteza kwa Paulo pamaso pa Festo ndi zomwe anagamula. (26:24-25) Ganizirani momwe Paulo anachitira kuti akope Agripa kuti akhale Mkhristu.</i> 6. <i>Ganizani za zomwe Paulo anayankha pa mawu a Agripa. (26:29)</i> <p>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze. Tsirizani Phunziro Lachitatu.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera B – Ku Kaisareya ndi mfumu.</p>
KUKUMBUTSANA	<p>Pangani posita ya mpingo ndipo mulembepo kuti: ‘Ungandikope kukhala Mkhristu?’</p>	<p>Lingaliraninso zomwe taphunzira ndipo kambiranani za mawu awa: ‘Kukopedwa ndi kwabwino kuposa kukakamidwa’. Mawu amenewa akugwirizana motani ndi zomwe taphunzira m’phunziroli?</p>
KHALANI MOYO UMENEWU	<p>Zomwe tikuphunzira m’phunziroli:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Ganizirani machitidwe a Paulo pa nkhani ya kulalikira uthenga mu ndime yomwe tawerengayi. Kodi ife tingasinthe ziti pa machitidwe amenewa? 2. Khalani ndi nthawi yoti ophunzira akambirane m’kalasi ndipo wophunzira mmodzi aziyankhula zofuna kukopa mnzake kuti akhale Mkhristu. 	<p>Zomwe tikuphunzira m’phunziroli:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Siyanitsani maganizo a atsogoleri Achiyuda ndi olamulira a Chiroma pa nkhani ya Uthenga Wabwino m’buku la Machitidwe. Kodi pamenepa tikuphunzira chiyani za momwe anthu amachitira akamva Uthenga Wabwino? 2. Ganizirani zomwe zikutilimbikitsa ife pa machitidwe akufotokoza ena Uthenga Wabwino.

	<p>A11 – KALASI Lachitatu Phunziro Lachinayi – Zochitika pa Maulendo a Paulo Mutu – ‘Ngozi ya sitima ya pamadzi’</p>	<p>A11 – KALASI Lachinayi Phunziro Lachinayi – Paulo m’Bwalo la Milandu Mutu – Kuonongeka kwa sitima ya pamadzi m’Nyanja ya Mchere</p>
	<p>Ndime Yowerenga: Machitidwe 27:13-14, 20-44 ndi 28:1-9 Vesi Yoloweza: Machitidwe 27:25</p> <p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Paulo akupita ku Roma kuti akazengedwe mlandu. 2. Mulungu amalonjeza kutithandiza pa zonse zomwe tikukumana nazo pa moyo wathu. 3. Zolinga za Mulungu zimakwaniritsidwa nthawi zonse. 	<p>Ndime Yowerenga: Machitidwe 27:1-44; 28:1-10 ndi 28-31 Vesi Yoloweza: Machitidwe 27:24-25</p> <p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Paulo akupita ku Roma kuti akazengedwa mlandu. 2. Mulungu amakhala akulamulira zonse zimene zimatchitikira ndipo amalonjeza kutithandiza. 3. Kukana Uthenga Wabwino kwa anthu ena, zotsatira zake ndi mwayi wa ena kumva Uthenga Wabwino.
<p>MAWU OYAMBA</p>	<ul style="list-style-type: none"> • Funsani ophunzira ngati alipo amene anakumana ndi namondwe pa nyanja. • Fufuzani momwe ankamvera mu mtima ndiponso ngati anapemphera kwa Mulungu kuti awapulumutse. • Konzekerani ndipo yambani kukambirana zomwe zinamuchitikira Paulo pamene sitima ya pamadzi inaonongeka. 	<ul style="list-style-type: none"> • Kambiranani nkhani ya kuchita mantha ndi ophunzira. • Afunseni afotokoze zomwe zinawachititsa mantha kwambiri. • Kambiranani za kufunika kwa malonjezo a Mulungu mu nthawi imene tikuchita mantha. (Salimo 23:4)
<p>KUTSIRIZA</p>	<p>Perekani Nkhani ya m’Baibulo</p> <p>Kambiranani ndi Kufotokoza:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Tsopano Paulo ali pa ulendo wopita ku Roma. Paulo akuwalangiza kuti asapitirize ulendowu nthawi yozizira koma palibe amene akumumvera. 2. Pa nyanja panayamba namondwe wamphamvu amene anatha masiku ambiri. Usiku wina Paulo anali ndi masomphenya ndipo anawuzidwa kuti anthu onse mu sitimamo adzapulumuka. Iye anafotokozera aliyense kuti anali ndi chikhulupiriro mwa Mulungu ndipo zonse zidzachitika monga momwe anamuwuziramo. 3. Kenaka iwo anafika kufupi ndi Melita, sitima yawo inagunda mchenga ndipo anthu onse 276 anatuluka ndi kupita pa gombe. 4. Anthu a ku Melita anawaonetsa chifundo chachikulu ndipo Paulo anachita zodabwitsa pa chilumbachi. 5. <i>Tsindikani momwe Mulungu analimbikitsira Paulo nthawi ya namondweyi.</i> 6. <i>Tsindikani kuti Akhristu sikuti sangakumane ndi zovuta pa moyo wawo.</i> 7. <i>Ganizirani momwe ife tingachitire pamene tikudutsa mu namondwe wa moyo wathu, tingathe kudziwa kupezeka kwa Ambuye ndi mphamvu zawo.</i> <p>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze. Tsirizani Phunziro Lachinayi.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera B – ‘Ngozi ya sitima ya pamadzi’.</p>	<p>Perekani Nkhani ya m’Baibulo</p> <p>Kambiranani ndi Kufotokoza:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Tsopano Paulo ali pa ulendo wopita ku Roma. Iwo anali akukumana ndi zovuta ku Krete. Choncho Paulo anawalangiza kuti asayambe ulendo wawo koma palibe amene anamumvera. 2. Pa nyanja panali namondwe wamphamvu kwambiri amene anatha masiku ambiri. Oyendetsa sitima anataya mtima za kuti angapulumuke. 3. Usiku wina Paulo anali ndi masomphenya ndipo anawuzidwa kuti aliyense mu sitimamo adzapulumuka. Iye anawuza anthuwo kuti anali ndi chikhulupiriro mwa Mulungu ndipo kuti zilizonse zidzachitika monga mmene Mulungu wayankhulira. Atha masiku khumi ndi anayi osadya Paulo anawalimbikitsa kuti adye ndipo kenaka anayandikira ku mtunda. 4. Kenaka iwo anafika kufupi ndi Melita ndipo anthu onse 276 anatuluka ndi kupita pa gombe. 5. Anthu a ku Melita anawaonetsa chifundo chachikulu ndipo Paulo anachita zodabwitsa pa chilumbachi. 6. Kenaka anakafika ku Roma, ndipo Paulo anayikidwa m’ndende ya m’nyumba koma anali ndi mpata wowuza anthu za Ambuye Yesu. 7. <i>Tsindikani momwe Mulungu analimbikitsira Paulo nthawi ya namondwe.</i> <p>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze. Tsirizani Phunziro Lachinayi.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera B – Kuonongeka kwa sitima ya pamadzi m’Nyanja ya Mchere.</p>
<p>KUKUMBUTSANA</p>	<ol style="list-style-type: none"> 1. Funsani ophunzira kuti adzitenge iwowo kukhala ngati Paulo. 2. Afunseni kuti alembe kalata kwa mnezawo amene ali pa mavuto ndipo amufotokozere momwe Mulungu anawathandizira nthawi yawo ya namondwe pamene ankapita ku Roma. Agwiritse ntchito zowachitikira polimbikitsa mnezawoyo. 	<ol style="list-style-type: none"> 1. Kumbutsanani zochitika pa moyo wa Paulo zomwe mwaphunzira ndipo onani za kukhulupirika kwa Mulungu komwe kukuoneka pa moyo wake. 2. Yang’anani tanthauzo la mawu alkuti “kupirira”. Kodi izi zikuoneka motani m’moyo wa Paulo? Limbikitsani ophunzira kuti aone zomwe zikufanana ndi zochitika kwa Paulo pa moyo wawo.
<p>KHALANI MOYO UMENEWU</p>	<p>Zomwe tikuphunzira m’phunziroli:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Funsani momwe kuonongeka kwa sitima yomwe Paulo anakwera kumalimbikitsira ife. 2. Kodi ndi maphunziro ati amene tingapeze kuchokera mu nkhani zina za m’Baibulo za momwe Mulungu anapulumutsira anthu mu nthawi zawo zovuta? Monga Yosefe, Danieli ndi ena ambiri. 3. Konzani pemphero la kuyamika Mulungu chifukwa cha ulumuliro wake pa moyo wathu. 	<p>Zomwe tikuphunzira m’phunziroli:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Tsindikani kuti Akhristu amakumananso ndi zovuta pa moyo wawo. 2. Kambiranani kuti nthawi imene tikudutsa mu namondwe wa moyo wathu, tingathenso kuzindikira za kupezeka kwa Ambuye. Onani Yesaya 43:2.

	<p>A12 – KALASI Lachitatu Phunziro Loyamba – Khristmasi Yoyamba Mutu – Zosatheka!</p>	<p>A12 – KALASI Lachinayi Phunziro Loyamba – Kubadwa kwa Mpulumutsi Mutu – Mauthenga a mngelo</p>
	<p>Ndime Yowerenga: <i>Luka 1:5-20 ndi 57-66</i> Vesi Yoloweza: <i>Luka 1:37</i></p> <p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Zakariya ndi Elizabeti anali okalamba pamene Mulungu anayankha mapemphero awo. 2. Palibe chinthu chosatheka ndi Mulungu. 	<p>Ndime Yowerenga: <i>Matayu 1:18-25; Luka 1:26-38</i> Vesi Yoloweza: <i>Matayu 1:21</i></p> <p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Mngelo anayankhula za kubadwa kwa Yesu mwachindunji pamene anawuza Yosefe zonse za moyo wake. 2. Mariya anawuzidwanso kuti adzakhala ndi mwana mwa mphamvu ya Mzimu Woyera.
<p>MAWU OYAMBA</p>	<ul style="list-style-type: none"> • Yankhulani zakuti nthawi zina anthu amadikira kwa kanthawi kuti Mulungu ayankhe mapemphero awo. • Fotokozani momwe Zakariya ndi Elizabeti analili ndi za kudikira kwawo kwa nthawi yayitali kuti pemphero lawo liyankhidwe zomwe zinkaoneka kuti ndi zosatheka. 	<ul style="list-style-type: none"> • Taganizani momwe amalengezera zinthu zofunika kwambiri pa dziko lapansi, makamaka pamene zangochitika kumene. Komatu palibe amene angalengeze molunjika zinthu zisanachitike. • Koma Mulungu angathe! Yosefe ndi Mariya anapatsidwa mauthenga ochokera kwa Mulungu za kubadwa kwa Ambuye Yesu, Iye asanabadwe.
<p>KUTSIRIZA</p>	<p>Perekani Nkhani ya m’Baibulo</p> <p>Kambiranani ndi Kufotokoza:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Fotokozani kuti Zakariya ndi Elizabeti ankafuna ana. Kumbutsani ophunzira manyazi ndi kunyozedwa kumene anthu opanda ana anakumana nako ku mayiko a kummawa mu nthawi ya Baibulo. 2. Zakariya anali ndi mwayi wogwira ntchito ngati wansembe m’Nyumba ya Mulungu. 3. Mngelo anaonekera kwa iye ndipo Zakariya anachita mantha. Kenaka mngeloyo anamuwuzwa kuti Elizabeti adzabereka mwana wamwamuna amene adzakhala wamkulu pamaso pa Ambuye ndipo adzathandiza anthu kuti akonzekere kubwera kwa Ambuye. (<i>Luka 1:17</i>) 4. Zakariya akuyankha kuti iwo ndi okalamba kwambiri kuti abereke ana. Mngelo anati popeza sanakhulupirire Mawu a Ambuye, iye sadzatha kuyankhula kapena kumva mpaka izi zitachitika. 5. Pamene mwana anabadwa Elizabeti anati adzatchedwa Yohane ndipo Zakariya anachitira umboni polembe dzinalo. Iye atangolemba dzinalo anayamba kuyankhula ndipo anadzazidwa ndi Mzimu Woyera ndi kunenera zonse zimene Yohane adzachte. 6. <i>Fotokozani zomwe anansi awo anayankhula, ndi zina zambiri. (1:65-66)</i> 7. <i>Siyantsani yankho la Elizabeti pa uthenga wa mngelo ndi yankho la Zakariya. Kodi pamenepa tikuphunzira chiyani?</i> <p>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze. Tsirizani Phunziro Loyamba.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera B – Zosatheka!</p>	<p>Perekani Nkhani ya m’Baibulo</p> <p>Kambiranani ndi Kufotokoza:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Mariya ndi Yosefe anali pa ubwenzi woti akwatirane. Kenaka Mariya analandira uthenga kuchokera kwa mngelo wa kuti iye adzabereka mwana wa mwamuna mwa mphamvu ya Mzimu Woyera. 2. Pamene Yosefe anamva zimenezi anafuna kumusiya mwamseri. Koma anawuzidwa m’maloto za kubadwa kwa Mwana amenewu, chifukwa chomwe akubadwira ndi ulosi umene udzakwaniritsidwe Iye akabadwa. 3. <i>Fotokozani za mwambo wa chinkhoswe mu chikhaliidwe cha Chiyuda.</i> 4. Yosefe ndi Mariya onse anakhulupirira uthenga umene analandira, ndipo momwe Yosefe analangizidwira anamutcha mwanayo Yesu “chifukwa adzapulumutsa anthu ake ku machimo awo”. 5. <i>Kambiranani mafunso atatu awa: a) N’chifukwa chiyani Yesu anabadwa modabwitsa mwa mphamvu ya Mzimu Woyera osati monga mmene zimachitikira? b) N’chifukwa chiyani Mariya ndi Yosefe anasankhidwa kukhala makolo ake pa dziko lapansi? (Onani m’ndandanda wa makolo awo - Matayu 1 ndi Luka 3.) c) N’chifukwa chiyani Mulungu anasankha kutumiza Mwana wake ku dziko lapansi?</i> <p>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze. Tsirizani Phunziro Loyamba.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera B – Mauthenga a mngelo.</p>
<p>KUKUMBUTSANA</p>	<p>Pa mutu wa “Zosatheka kukhala zotheka” lolani ophunzira alembe zinthu zimene zinachitikadi (makamaka zitsanzo za m’Baibulo) ngakhale zinkaoneka kuti zinali zosatheka. Pansi pake lembeni kuti: “Mulungu zikomo!”</p>	<ol style="list-style-type: none"> 1. Kodi Mulungu anayamba wakuwuzani inu kapena kuwuzwa mzanu uthenga umene unali wovuta kuwukhulupirira ndi kuwudalira? 2. Kodi m’Baibulo tawerenga maukosi otani a phunziro lino amene anakwaniritsidwa pamene Yesu anabwera?
<p>KHALANI MOYO UMENEWU</p>	<p>Zomwe tikuphunzira m’phunziroli:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Kodi mwaphunzira chiyani kuchokera m’phunziroli? 2. Ganizirani za kufunika kopitiriza kupemphera, ngakhale zikoneka ngati yankho silibwera msanga. 3. Ganizirani za kufunika kwa kudalira Mawu a Mulungu, Baibulo, ngakhale kuti zinthu zina zimaoneka ngati ndi zosatheka. 	<p>Zomwe tikuphunzira m’phunziroli:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Kodi ndi ziti kuchokera m’phunziro la lero zomwe tingazigwiritse ntchito pa moyo wathu? 2. Kodi kufunika kwa kubwera kwa Ambuye Yesu kwa ife ndi kotani? 3. Konzani mapemphero oyamika chifukwa cha zonse Mulungu anachita potumiza Mwana wake. Onani 2 Akorinto 9:15.

	A12 – KALASI Lachitatu Phunziro Lachiwiri – Khristmasi Yoyamba Mutu – Ntchito ya padera	A12 – KALASI Lachinayi Phunziro Lachiwiri – Kubadwa kwa Mpulumutsi Mutu – Lamulo la Kaisara
	<p>Ndime Yowerenga: <i>Luka 1:26-38</i> Vesi Yoloweza: <i>Luka 1:38</i></p> <p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ol style="list-style-type: none"> Mariya ndi Yosefe anali anthu apadera kwambiri, amene Mulungu anawagwiritsa ntchito mwapaderanso. Kubadwa kwa Yesu, Mwana wa Mulungu, kunali kodabwitsa. 	<p>Ndime Yowerenga: <i>Luka 2:1-7</i> Vesi Yoloweza: <i>Luka 2:7</i></p> <p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ol style="list-style-type: none"> Ufumu wa Chiroma unali ndi atsogoleri amene ankatchedwa Akaisara. Kaisara analamula kuti kukhale kalemba zomwe zinachititsa Mariya ndi Yosefe kuti apite ku Betelehemu kukalembetsa. Izi zinachitika pofuna kukwaniritsa ulosi wa Chipangano Chakale.
MAWU OYAMBA	<ul style="list-style-type: none"> Kambiranani za chinthu choyamba kuchita pamene mwana wabadwa ndi kumupatsa dzina. Yesu ali ndi mayina ambiri. Onaninso mbiri yonse yonena za kubadwa kwa Yesu mu <i>Luka 1 ndi 2, ndi Mateyu 1 ndi 2</i> ndipo lembani ena mwa mayina ake. Ndi dzina liti lomwe mumalikonda nanga ndi chifukwa chiyani? 	<ul style="list-style-type: none"> M'magulu aang'ono, lembani mayina a malo onse amene atchulidwa mu Ndime Yowerenga. Chitaninso chimodzimidzi ndi mayina a anthu. Tsimikizani za mayankho anu powerenganso Ndime Yowerenga.
KUTSIRIZA	<p>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</p> <p>Kambiranani ndi Kufotokoza:</p> <ol style="list-style-type: none"> Mariya ndi mtsikana amene ali pa ubwenzi ndi Yosefe. Mngelo Gabrieli wabwera kudzamuchezera ndipo akudabwa kwambiri pamene wamva kuti Ambuye wakukomerani mtima kwambiri. Mngelo akumuwaza kuti adzabereka mwana amene dzina lake ndi Yesu. Iye ndi Mwana wa Wammwambamwamba ndipo adzakhala pa mpando waufumu wa Davide. Mariya akudabwa kwambiri papeza anali namwali koma mngelo akumufotokozera kuti adzakhala ndi mwana mwa mphamvu ya Mzimu Woyera. Yankho la Mariya ndi lodabwitsanso ndipo akuti, "Zichitike kwa ine monga mwanenera." <i>Kambiranani za zinthu zimene mukuganiza kuti zinali m'maganizo mwa Mariya pamene mngelo anamuwaza kuti Ambuye wakukomerani mtima kwambiri ndi kuti adzabereka mwana. Onaninso vesi 46 ndi 47.</i> <i>"Pakuti palibe chinthu chosatheka ndi Mulungu." Ganizirani za ana ena amene ali m'Baibulo amene anabadwa mosayembekezeka ndi anthu.</i> <p>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze. Tsirizani Phunziro Lachiwiri.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera B – Ntchito ya padera.</p>	<p>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</p> <p>Kambiranani ndi Kufotokoza:</p> <ol style="list-style-type: none"> Mariya pamodzi ndi Yosefe anali zidzukululu za Mfumu Davide choncho pamene analamula kuti pakhale kalemba, iwo anayenera kupita ku Betelehemu. Uwu unali ulendo wa makilomita makumi asanu ndi awiri ndipo unali ovuta kwambiri kwa Mariya amene anali woyembekezera. Nthawi imeneyi mu Betelehemu munali anthu ochuluka kwambiri, choncho anayenera kupeza malo m'khola la ng'ombe kapena m'phanga. Kumeneku Yesu anabadwira m'malo wamba, malo a anthu osauka. Taganizirani za zinthu zingapo zomwe zinachitika kuti Yesu abadwire mu Betelehemu monga momwe Mika analosera ndiponso muone kuopsa kwa mphamvu ya Mulungu kuti zonse zichitike monga analosera. (<i>Mika 5:2</i>) <i>Werengani Yohane 3:16 ndi Agalatiya 4:4 kuti mupeze matanthauzo a mavesi amenewa kuti zithandize aliyense kumvetsetsa zochitikazi.</i> <p>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze. Tsirizani Phunziro Lachiwiri.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera B – Lamulo la Kaisara.</p>
KUKUMBUTSANA	<p>Yankhani mafunso awa:</p> <ol style="list-style-type: none"> Kodi mngelo dzina lake anali ndani? Kodi Mariya anachita chiyani atangomva uthengawu? Kodi mngelo anamulonjeza chiyani Mariya? Kodi iye anachita chiyani atamva lonjezo limeneli? (<i>1:38</i>) Kodi atamva nkhani imeneyi anachita chiyani pambuyo pake? (Onani <i>vesi 46 ndi 47</i>.) 	<p>Yankhani mafunso awa:</p> <ol style="list-style-type: none"> Tchulani dzina la mzinda umene unali makilomita makumi asanu ndi awiri kuchokera kumene ankakhala. Kodi ophunzira angafune kuyenda mtunda umenewu motani, ngakhale ali wosayembekezera? Kodi kusiyana kwa zochitika pa kubadwa kwa Yesu ndi kubadwa kwa ana athu lero n'kotani? chomwe munakafuna kuonjezera kapena kusintha? Kodi kutumikira Yehova kungasinthe motani moyo wanu lero?
KHALANI MOYO UMENEWU	<p>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</p> <ol style="list-style-type: none"> M'magulu aang'ono lembani mayina a malo onse amene atchulidwa mu Ndime Yowerengayi. Chitaninso chimodzimidzi ndi mayina a anthu. Onaninso kuti musasiye chilichonse mu ndime imeneyi. Ganizirani kufunika kwa chilichonse chimene chalembedwa. 	<p>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:</p> <p>Kambiranani za kubwera kwa Yesu m'dziko lapansi ndi momwe kwakhudzira mbiri ya anthu ndi momwe zikukhudzira miyoyo yathu.</p>

	A12 – KALASI Lachitatu Phunziro Lachitatu – Khrismasi Yoyamba Mutu – Mu Betelehemu	A12 – KALASI Lachinayi Phunziro Lachitatu – Kubadwa kwa Mpulumutsi Mutu – Kubwera kwa abusa
	<p>Ndime Yowerenga: <i>Luka 2:1-20</i> Vesi Yoloweza: <i>Luka 2:11</i></p> <p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ol style="list-style-type: none"> Chinali chikonzero cha Mulungu kuti Yesu abadwe mwaumphawi ndi movuta. Mulungu ndiye ankalamulira zochitika zonse ndipo akuterobe mpaka lero. 	<p>Ndime Yowerenga: <i>Luka 2:8-20</i> Vesi Yoloweza: <i>Luka 2:11</i></p> <p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ol style="list-style-type: none"> Mngelo anaonekera kwa abusa pamene ankaweta nkhosa zawo. Iwo anakhulupirira zomwe anamva ndipo ananyamuka kukaona.
MAWU OYAMBA	<ul style="list-style-type: none"> Funsani ophunzira kuti atchule zina mwa zazikulu zomwe zinachitika m'mbiri ya dziko lapansi. Fotokozani kuti kubwera kwa Mwana wa Mulungu chinali chinthu chachikulu kwambiri. Lembani mwandondomeko kuti muonetse zonse zimene zinachitika mu mdime imeneyi. 	<p>M'magulu ang'onoang'ono chitani sewero kuchokera pa ndime imeneyi. Gwiritsani ntchito tinsalu kukhala ngati zofunda za abusa.</p>
KUTSIRIZA	<p>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</p> <p>Kambiranani ndi Kufotokoza:</p> <ol style="list-style-type: none"> Mariya pamodzi ndi Yosefe anali zidzukululu za Mfumu Davide, choncho pamene analamula kuti pakhale kalemba, iwo anayenera kupita ku Betelehemu. Uwu unali ulendo wa makilomita makumi asanu ndi awiri ndipo unali ovuta kwa Mariya amene anali woyembekezera. Nthawi imeneyi mu Betelehemu munali anthu ochuluka kwambiri, choncho anayenera kupeza malo m'khola la ng'ombe kapena m'phanga. Kumeneku Yesu anabadwira m'malo wamba, malo a anthu osauka. Ife tikuganiza kuti Yesu anabadwa usiku ndipo abusa ndi anthu ena ochepa anali asanagone. Iwo analandira uthenga wa kubadwa kwa Mpulumutsi - Khristu Ambuye. Gulu lalikulu la angelo linaonekera kwa abusa, likutamanda Mulungu. Abusa ananyamuka ndi kupita ku Betelehemu kuti akaone zomwe zinachitikazo. Iwo anapeza Mariya ndi Yosefe pamodzi ndi mwanayo. Iwo anafalitsa nkhani yonse ya zimene anaona ndipo anabwerera akuyamika ndi kutamanda Mulungu <i>Fotokozani za malonje oyamba a angelo amene analembedwa apa komanso ndi pamalo pena m'Baibulo.</i> <i>Kambiranani za anthu awiri amene anali omvera pa ulendo wawo.</i> <i>Kambiranani zomwe tikuphunzira kuchokera pa nkhani ya abusawa.</i> <p>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze. Tsirizani Phunziro Lachitatu.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera B – Mu Betelehemu.</p>	<p>Perekani Nkhani ya m'Baibulo</p> <p>Kambiranani ndi Kufotokoza:</p> <ol style="list-style-type: none"> Ife tikuganiza kuti Yesu anabadwa usiku ndipo abusa ndi anthu ena anali asanagone. Iwo analandira uthenga wa kubadwa kwa Mpulumutsi - Khristu Ambuye. Gulu lalikulu la angelo linaonekera kwa abusa likutamanda Mulungu. Abusa ananyamuka kupita ku Betelehemu kuti akaone zomwe anamvazo. Iwo anapeza Mariya ndi Yosefe pamodzi ndi mwanayo. Iwo anafalitsa nkhani yonse ya zimene anaona ndipo anabwerera akuyamika ndi kutamanda Mulungu. <i>Kambiranani zomwe tikuphunzira kuchokera pa nkhani ya abusawa.</i> <i>Kambiranani za kuti Mulungu kudzera mwa angelo anaonekera kwa anthuwa akugwira ntchito. Lero lye angathe kuyankhula nafe pamene tikugwira ntchito zathu za tsiku ndi tsiku.</i> <i>Tikamva zomwe Mulungu watichitira ife, tikuyenera kuwawuzanso anzathu.</i> <p>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze. Tsirizani Phunziro Lachitatu.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera B – Kubwera kwa abusa.</p>
KUKUMBUTSANA	<p>Yankhani mafunso awa.</p> <ol style="list-style-type: none"> Kodi mukuganiza kuti ndi chifukwa chiyani angelo amalonjera anthu monga anachitira pa vesi 10? Kodi mukuganiza kuti Mulungu amayankhula kwa anthu wamba lero monga abusawa? N'chifukwa chiyani / ngati si choncho n'chifukwa chiyani? Kodi mukuganiza kuti Mariya ankaganiza chiyani? (2:19) Kodi abusa anachita chiyani atabwerera komwe kunalo nkhosa zawo? 	<p>Yankhani mafunso awa.</p> <ol style="list-style-type: none"> Kodi inu mukuganiza kuti ndi chifukwa chiyani abusa anachita mofulumira angelo aja atachoka? Abusa anadalitsidwa chifukwa chochita mofulumira. Kodi mungalembe vesi 20 m'mawu a lero? Kodi mukuganiza kuti Mariya ankaganiza chiyani? (2:19)
KHALANI MOYO UMENEWU	<p>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli: Yerekezani kuti ndinu abusa. Kugwiritsa ntchito mavesi 8-17 lembani m'ndandanda wa zochitika wa zomwe mwamva, kuziona ndi kuzikhudza.</p>	<p>Fotokozani zofuna kukhala ndi m'ndandanda wa zomwe Mulungu akuyankhula kwa inu ndi kumalemba tsiku lake kuti tsiku lina mukadzaona zimenezi mudzalimbikitsidwe pa moyo wanu.</p>

	<p>A12 – KALASI Lachitatu Phunziro Lachinayi – Khristmasi Yoyamba Mutu – M’nyumba ya Mulungu</p>	<p>A12 – KALASI Lachinayi Phunziro Lachinayi – Kubadwa kwa Mpulumutsi Mutu – Mphatso za anzeru a kummawa</p>
	<p>Ndime Yowerenga: <i>Luka 2:22-40</i> Vesi Yoloweza: <i>Luka 2:30</i></p> <p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Simeoni ndi Ana anasangalala pamene Yesu anabadwa chifukwa iwo ankamvetsa kufunika kwake. 2. Ndi zofunika kuyamika Mulungu chifukwa chotumiza Yesu pa dziko lapansi. 	<p>Ndime Yowerenga: <i>Mateyu 2:1-23</i> Vesi Yoloweza: <i>Mateyu 2:11</i></p> <p>Ife tikuphunzira kuti:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Anthu awa ankamvetsetsa kuti Yesu anali munthu wapadera kwambiri. 2. Ngakhale Anzeruwa anabweretsa chuma chawo, Yesu ndiye anali chuma chenicheni.
<p>MAWU OYAMBA</p>	<ul style="list-style-type: none"> • Ganizani za chisangalalo chimene chimakhalapo mwana akabadwa. • Kodi kusiyana kwa kubadwa kwa Yesu kunali kotani? • Fotokozani zomwe Lamulo la Chiyuda linkanena kuti makolo ankayenera kupita ndi mwana wawo ku Nyumba ya Mulungu kuti akapereke nsembe ya kuyeretsedwa kwa mayi ndi ya kuyamika Mulungu. (<i>Levitiko 15</i>) 	<ul style="list-style-type: none"> • Ganizani za chisangalalo chimene chimakhalapo mwana akabadwa. Ganizirani za abale ndi abwenzi amene amabwera kudzaona mwana watsopano. • Fotokozani za Anzeru a Kummawa ndi za kutalika kwa mtunda umene anayenda. • Fotokozani kuchokera pa nkhanayi kuti Mulungu ankachita zinthu motsogola Satana asanachite zake Perekani zitsanzo kuchokera mu ndime imeneyi.
<p>KUTSIRIZA</p>	<p>Perekani Nkhani ya m’Baibulo</p> <p>Kambiranani ndi Kufotokoza:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Yesu atabadwa anapita naye ku Nyumba ya Mulungu ku Yerusalemu. 2. Mariya ndi Yosefe onse anawuzidwa kuti dzina la mwanayo ndi Yesu. Tsopano akupereka nsembe monga mwa Lamulo. 3. Iwo akumana ndi Simeoni amene anawuzidwa kuti sadzafa mpaka ataona “Khristu wa Ambuye”. 4. Iye ananyamula mwanayo m’manja mwake ndipo anayamika Mulungu chifukwa anzindikira kuti Yesu anali Mpulumutsi. 5. Iwo anakumananso ndi mayi wokalamba wotchidwa Ana, amenenso anayamika Mulungu ndi “kuyankhula za Mwanayo kwa onse amene ankayembekezera chipulumutso cha Yerusalemu.” 6. <i>Fotokozani momwe Simeoni ndi Ana anadziwira kuti Yesu anali munthu wapadera kwambiri.</i> 7. <i>Kambiranani zomwe ananena kuti zidzachitika kwa Yesu. (Onani mavesi 31-32, 34, 35, ndi 38.)</i> <p>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze. Tsirizani Phunziro Lachinayi.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera B – M’nyumba ya Mulungu.</p>	<p>Perekani Nkhani ya m’Baibulo</p> <p>Kambiranani ndi Kufotokoza:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Anzeru a Kummawa anaona nyenyezi ndipo kuchokera pa zimene ankaphunzira anzindikira kuti kwabadwa mfumu yatsopano ndipo anafuna kupita kukapereka ulemu. 2. Iwo anafika ku nyumba yaufumu ya Herode mu Yerusalemu, poganiza kuti mfumu yatsopano inali kumeneko. 3. Herode anasautsika mu mtima podziwa kuti tsopano pali wina womutsutsa, koma atsogoleri achipembedzo anamuwuzza zomwe zinali m’buku la Mika (<i>Mika 5:2</i>) za kubadwa kwa Mfumu mu Betelehemu. 4. Anzeru a Kummawa apita ku Betelehemu, apeza Mwana kumeneko, iwo amupatsa chuma chawo ndi kumupembeda. 5. Iwo anachenjedzewa m’maloto usiku kuti abwerere kwawo podzera njira ina ndipo asakamuwuzze Herode kuti amupeza mwanayo. 6. Yosefe wawuzidwa kuti atenga Mariya ndi mwanayo apite ku Igupto kuti akabisale. 7. Herode wazindikira kuti amunamiza anthu aja ndipo walamula kuti akaphe mwana aliyense wamwamuna mu Betelehemu kuyambira wamng’ono mpaka wa zaka ziwiri. 8. Kenaka Yosefe anawuzidwa kuti abwerere ndipo anakakhala ku Nazareti. 9. <i>Ganizirani momwe Mulungu anakonzera zinthu zonse zaka mazana ambiri apitawo poneneratu mu maulosi awa. (Onani mavesi 5-6, 15, 17-18, ndi 23.)</i> 10. <i>Ganiziranso momwe Herode ankagwirira ntchito ya Satana.</i> <p>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze. Tsirizani Phunziro Lachinayi.</p> <p>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera B – Mphatso za anzeru a kummawa.</p>
<p>KUKUMBUTSANA</p>	<ul style="list-style-type: none"> • Simeoni ananena kuti iye adzakhala Kuunika. M’magulu ang’onoang’ono kambiranani za ubwino wa kuunika. • Kodi iwo adzaona motani vesi 32 kusiyana ndi mmene akuonera tsopano? • Limbikitsani ophunzira kuti apemphere kwa Mulungu kuti awatumizire kuunika kwakukulu m’miyoyo yawo. Alimbikitseni kuganizira za madera ofunika kwambiri omwe akufunika kuti athandizidwe ndipo apempherere madera amenewo. 	<ol style="list-style-type: none"> 1. Fotozani matanthauzo a mphatso zimene anapereka kwa Yesu - Golide akuonetsa kuti iye ndi Mfumu, Mure akuonetsa kuti iye ndi Mpulumutsi amene adzasautsidwa ndi kufa, ndipo Lubani akuonetsa kuti iye ndi Mulungu amene tikuyenera kumulambira. 2. Kambiranani zonse zimene zikusonyeza kuti Yesu ali ngati chuma, mphatso yaulere kwa aliyense amene angamulandira kukhala Mpulumutsi ndi Ambuye wake.
<p>KHALANI MOYO UMENEWU</p>	<p>Zomwe tikuphunzira m’phunziroli:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Kodi ndi chiyani chomwe tingaphunzire ndi kuti ophunzira achigwiritse ntchito pa miyoyo yawo? 2. Kumbukirani kuti chipulumutso chimatanthauzanso kukhala wangwiro ndipo si chinthu chochitika nthawi imodzi koma ndi ntchito ya moyo wonse wa munthu. 	<p>Zomwe tikuphunzira m’phunziroli:</p> <ol style="list-style-type: none"> 1. Ganizirani mphatso zomwe tingapite nazo kwa Ambuye Yesu monga chopereka. 2. Lembani zitsanzo za tsiku ndi tsiku za zomwe Satana amachita monga Mdierekezi. Chenjerani ndi momwe iye magwirira ntchito zake.

Malangizo a Aphunzitsi a Kachongedwe ka Maphunziro

Maphunziro a Kalasi Lachitatu

- Ophunzira sangatsirize maphunziro awa popanda kuwerenga Baibulo ndipo akuyenera kuwerenga ndime imodzi kapena zambiri.
- Kafunsiwe n'kosiyanasiyana, pena pali mabokosi, pena pali mawu amene akusowa ndi njira zina zambiri.
- Mafunso akonzedwa kuti aziyankhidwa kuchokera m'baibulo la Mawu a Mulungu mu Chichewa Chalero ndi Buku Lopatulika ndi Mawu a Mulungu.
- Cholinga chathu n'chakuti ophunzira onse, kaya akugwiritsa Baibulo la mtundu wanji, azitha kuyankha mafunso.
- Sabata lililonse lili ndi marikisi 20 ndipo pa mwezi pali marikisi 80, ngati munthu wakhonza bwino maphunziro onse.
- Kalasi Lachitatu - Pali marikisi imodzi pa yankho, monga momwe tasonyezera.

Maphunziro a Kalasi Lachinayi

- Awa ndi maphunziro ovutirapo kusiyana ndi Maphunziro a Kalasi Lachitatu.
- Muli mafunso ovutirapo ofuna mayankho.
- Marikisi 20 pa sabata ndi marikisi makumi 80 pa mwezi ngati amaliza maphunziro molondola ndiponso mafunso onse ali ndi mayankho ake.

FUNDO ZA KACHONGEDWE

Choyamba aphunzitsi akupemphedwa kuti:

- Onani phunziro lililonse ndipo chongani moyenera zolondola kapena zolakwitsa.
- Perekani marikisi amene mwalangizidwa kutero.
- Nthawi zonse chongani pogwiritsa ntchito mitundu yosiyana ya zolemba, CHONGANI yankho lolondola.
- Lembani yankho lolondola poyenera kutero ndi kukonza mawu olakwika kalembedwe ake, koma MUSACHOTSE marikisi.
- Perekani marikisi ochepa pa yankho lolondola mbali imodzi yokha.
- Phatikizani marikisi onse a pa mwezi ndipo lembani kumapeto pa malo amene mwapatsidwa.

N'kofunika kusaumira ndi kuchita chilichonse chothandiza kulimbikitsa ophunzira kuti aphunzire Baibulo lawo. N'zothandizanso kuti kumapeto kwa mwezi uliwonse mphunzitsi azilemba mawu a chilimbikitsa kwa wophunzira pa malo amene aperekedwa. Mutha kulemba ndemanga yoyamikira kuchekenira bwino, zilembo zabwino ndi kumvetsa bwino phunziro ndi zina zambiri.

Yesetsani kuti ndemanga, mafunso, ziganizo, zomwe mwaona ndi zina zambiri zikhale zosiyanasiyana, kuti zithandize kupanga zinthu kukhala zosiyana. Izi zimafunika kuganiza bwino, ndipo ndi kofunika kuti wophunzira azikhala ndi chidwi nthawi zonse. Ngati chiganizo chomwecho kapena funso lomwe likubwera mwezi uliwonse, zimachotsa chidwi cha wophunzira.

KALASI Lachitatu

Ndemanga zina

"Ntchito yabwino kwambiri! Inu munamvetsa bwino mafunso onse. Ine ndasangalala ndi yankho la funso lotsiriza limene mwaliyankha bwino kwambiri."

"Moni Yonatani. Ndikuyamika chifukwa cha kulimbikira kwako. Ndi zosangalatsa kwambiri kuti wayesetsa kuyankha mafunso onse. Ine ndalembe mayankho a mafunso ena amene sunayankhe."

Ndemanga zauzimu

"Mose anali ndi mavuto ndi ana a Israeli, koma Mulungu sanamusiye yekha kuti athetse mavutowo."

"Yosefe sanayiwale kuti abambo ake anamuphunzitsa kukonda Mulungu. Iye anakumbukira zimenezi ngakhale anali kutali ndi kwawo."

"Bartimeyu anatsimikiza mtima zofuna kulandira kuchokera kwa Ambuye Yesu. Iye sanakhumudwitsidwe chifukwa tsopano ankatha kuona ndipo anadziwa kuti Ambuye Yesu anali munthu wapadera kwambiri."

KALASI Lachinayi

Ndemanga zina

"Maphunziro enanso abwino kwambiri. Zikuoneka kuti tsopano ukumvetsa bwino Nkhani za m'Baibulo ndipo ndikukhulupirira kuti wasangalala nazo. Zikomo kwambiri chifukwa chokhala ndi nthawi yokwanira yochita mosamala maphunzirowa. Zikanatheka kuchita mofulumira, choncho ine ndi kuyamika kwambiri."

"Rakele, wayesetsa ndithu. Ine ndikaona mayankho akowa, zikuonetsa kuti sunamvetse bwino Nkhani za m'Baibulo. Bwanji uwerengenso zimenezi."

Ndemanga zauzimu

"Mafanizo nthawi zina amatchedwa nkhanu wamba koma zokhala ndi matanthauzo akumwamba kapena ozama. Kodi ungaganizire tanthauzo lozama la fanizo lomwe lili mu Phunziro 3?"

"Stefano anafa imfa yowawa kwambiri, koma iye sanachite mantha ndi imfa, chifukwa ankadziwa kuti anali ndi Mulungu, ndipo ankadziwa kuti akakhala ndi Ambuye Yesu kumwamba."

Zoonjezera A - Kalasi Lachitatu Zinthunzi Zaulelele m'Baibulo

	Mutu	Nkhani m'Chithunzi
A7	Moyo wa Yakobo	Munthu wachinyengo
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/esau-jacob/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/jacob-deceives/
		Kamaloto
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/jacob-deceives/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/jacob-dream/
		Kukhumudwitsidwa
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/jacob-wedding/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-049-parable-sower/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/parable-sower/
		Kuzindikira kwake
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/jacob-returns/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/jacob-esau-reunited/
A8	Pemphero	Pemphero ndi chiyani?
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/david-psalms/
		Kodi Mulungu amamva mapemphero athu?
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/pharisee-tax-collector/
		Kodi tingapemphere motani?
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-036-lords-prayer/
		Kodi Mulungu amayankha pemphero?
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/samuel-born/
A9	Paulo	'Wozunza Akhristu'
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-conversion/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/bj-paul-maps/
		'Masautso ake'
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-conversion/
		'Paulo mlaliki'
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-cyprus/
		'Mzinda wogawanikana'
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-antioch-iconium/

Zoonjezera B - Kalasi Lachitatu Zinthunzi Zaulelele m'Baibulo

	Mutu	Nkhani m'Chithunzi
A10	Zochitika pa Maulendo a	Kuzunzika chifukwa cha Ambuye
	Paulo	https://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-antioch-iconium/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-lystra-derbe/
		Bwenzi la muyaya
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-antioch-philippi/
		https://www.freebibleimages.org/photos/bt-paul-lydia/
		Paulo m'ndende
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-silas-prison/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/bj-paul-maps/
		Mzinda wa Atene
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-thessalonica-berea/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-athens/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/athens/
A11	Zochitika pa Maulendo a	'Kugawana ndi anthu ena'
	Paulo	https://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-corinth/
		'Chiwembu chofuna kumupha'
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-arrested-jerusalem/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-felix/
		'Paulo pamaso pa mfumu'
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-festus-agrippa/
		'Ngozi ya sitima ya pamadzi'
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-shipwrecked/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-rome/
A12	Khrismasi Yoyamba	Zosatheka!
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/zechariah-elizabeth/
		https://www.freebibleimages.org/photos/zechariah-john/
		Ntchito ya padera
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-003-birth-announcement/
		https://www.freebibleimages.org/photos/mary-angel/
		Mu Betelehemu
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-007-birth-jesus/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/christmas-jesus-birth/
		https://www.freebibleimages.org/photos/jesus-birth/
		https://www.freebibleimages.org/photos/shepherds-angels/
		M'nyumba ya Mulungu
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/simeon-anna/
		https://www.freebibleimages.org/photos/simeon-anna-temple/

Zoonjezera A - Kalasi Lachinayi Zinthunzi Zaulelele m'Baibulo

	Mutu	Nkhani m'Chithunzi
A7	Yakobo	Munthu wachinyengo
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/esau-jacob/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/jacob-deceives/
		Wolota
		http://www.freebibleimages.org/illustrations/jacob-dream/
		Kukhumudwitsidwa
		http://www.freebibleimages.org/illustrations/jacob-wedding/
		http://www.freebibleimages.org/illustrations/jacob-returns/
		Kuzindikira
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/jacob-esau-reunited/
A8	Kukhala Mkristu	Kuphunzira za pemphero
		http://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-036-lords-prayer/
		http://www.freebibleimages.org/illustrations/jonah-disobeys/
		http://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-silas-prison/
		Kuphunzira mawu a Mulungu
		http://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-thessalonica-berea/
		http://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-last-days/
		http://www.freebibleimages.org/illustrations/jehoshaphat-reforms/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-ephesus-antioch/
		Kukhala moyo wokondweretsa Mulungu
		http://www.freebibleimages.org/photos/vineyards-watchtowers/
		Kupereka kwa Mulungu
		https://www.freebibleimages.org/photos/lumo-widow-mite/
A9	Mtumwi Paulo	Kusinthika kwake
		http://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-conversion/
		Maulendo ake
		http://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-cyprus/
		http://www.freebibleimages.org/illustrations/bj-paul-maps/
		Ulaliki wake
		http://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-antioch-iconium/
		Masautso ake
		http://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-antioch-iconium/

Zoonjezera B - Kalasi Lachinayi Zinthunzi Zaulelele m'Baibulo

	Mutu	Nkhani m'Chithunzi
A10	Paulo	Paulo ku Filipi
		https://www.freebibleimages.org/photos/bt-paul-lydia/
		https://www.freebibleimages.org/photos/bt-paul-fortune-teller/
		https://www.freebibleimages.org/photos/bt-paul-prison/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-antioch-philippi/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-silas-prison/
		Paulo ku Tesalonika ndi Bereya
		http://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-thessalonica-berea/
		http://www.freebibleimages.org/illustrations/bj-paul-maps/
		Paulo kwa Atene ndi ku Korinto
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/athens/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-athens/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-corinth/
		Paulo ku Efeso
		http://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-ephesus/
		http://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-demetrius-artemis/
A11	Paulo m'Bwalo la Milando	Yerusalemu ndi gulu la anthu
		http://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-jerusalem-return/
		http://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-arrested-jerusalem/
		Ku Kaisareya ndi abwanamkubwa
		http://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-felix/
		http://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-festus-agrippa/
		Ku Kaisareya ndi mfumu
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-festus-agrippa/
		Kuonongeka kwa sitima ya pamadzi m'Nyanja ya Mchere
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-shipwrecked/
		http://www.freebibleimages.org/illustrations/paul-rome/
A12	Kubadwa kwa Mpulumutsi	Mauthenga a mngelo
		https://www.freebibleimages.org/photos/joseph-angel/
		https://www.freebibleimages.org/photos/mary-angel/
		Lamulo la Kaisara
		https://www.freebibleimages.org/photos/jesus-birth/
		https://www.freebibleimages.org/photos/prophecies-birth-jesus/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/christmas-jesus-birth/
		Kubwera kwa abusa
		https://www.freebibleimages.org/photos/shepherds-angels/
		Mphatso za anzeru a kummawa
		https://www.freebibleimages.org/photos/wise-men/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-009-flight-egypt/
		https://www.freebibleimages.org/illustrations/bj-jesus-journeys/



© Bible Educational Services 2020

www.besweb.com

Registered Charity UK CIO 1186004

NY - 02/2023
(Chichewa)